M'BADWO WA MPINGO SARDE

Jeffersonville, Indiana, USA
DISEMBALA 9, 1960

1 … Mfumu. M'bale wanga amandiuza kuti panali … Mipango iyi inali ya munthu wina amene ali kufa ndi cancer. Choncho tikhala tikupempherera izi posachedwapa. [M'bale Neville akunena kuti, "Pali zopempha ziwiri cham'mbali inayo."] Zopempha ziwiri? Chabwino. Chabwino, bwana. Ndipo ndiziika apa kuti tizipempherereno.

2 Ndipo wina wangobweretsa chidziwitso, kubwera mozungulira kudzapereka chidziwitso monga choncho … zokhudzana ndi misonkhano ya mawa. Inu amene muli pano kudzatichezera, tikufuna tikutsimikizireni kuti tidzakhala wokondwa kukhala nanu mutabwera kumsonkhano kumasanaku. Pa 2 koloko mawa masana iwo adzakhala ndi misonkhano yomvera tepi. Ngati inu simukuchita kanthu kenakalikonse, padzakhala … umodzi wa mauthenga amene simunawamvepo udzakhala ukuseweredwa, ndipo tidzakhala ndi msonkhano wa pemphero, ndipo tikuyembekeza nthawi yabwino mawa masana pa 2 koloko. Idzakhala nthawi yotangwanika zedi kwa ine, chifukwa mawa, mwaona, ine ndiyenera kutenga Lamulungu m'mawa ndiponso Lamulungu usiku ndi mawa usikunso, ndi mbiri zonse za mipingo imeneyo.

3 Ndipo tsopano, Lamulungu m'mawa Ambuye akalola, tikuyembekezera nthawi yopambana, chifukwa Lamulungu m'mawa pokhala ndi khalidwe lakupumula kuchokera …. Loweruka usiku ndi M'badwo wa Mpingo wa Laodikaya. Koma Lamulungu m'mawa ndikufuna ndidzatenge za anamwali ogona, ndi chiukitsiro, awa 144,000, ndi zonse izo zocheperako zosalumikizika bwino zimene zimamangirira Uthenga pamodzi kwa Lamulungu m'mawa.

Misonkhano idzayamba 9 koloko. Ndizoona zimenezo, Abusa 9 koloko, Lamulungu m'mawa zimene … tikufuna kudzatenga zinthu zonse ngati izi: Ndichiyani chomwe chidzachitikire anamwali ogona? Ndichiyani chimene adzakhale anamwali ochenjera? Ndi

nthawi yanji yomwe abwererenso? Kapena ndikuti 144,000 adzawonekere? Ndi zinthu zambiri ngati zimenezo kwa Lamulungu m'mawa, kuyesa kuzimangiriza pamodzi izo - zotani, zimene zikupita molunjika pamodzi ndi Uthenga uwu. Ndipo Lamulungu usiku tidzakhala tikutenga za M'ngelo uyu wamkulu wotsiriza ndi Uthenga ku Laodikaya - Lamulungu usiku, Ambuye akalola.

4 Ndipo tsopano … ndipo mawa masana pali msonkhano pano, msonkhano womvetsera tepi. M'bale Gene amangondiuza ine kuti iwo adzakhala … tidzayamba 2 koloko mawa masana. Anthu inu amene mumakonda kubwera kudzamvera ma Uthenga, kukhala ndi pemphero mozungulira guwa, inu amene mukusakasaka Mzimu Woyera kapena chinachake - nthawi yodabwitsa. Kachisi alibwino ndi wofunda, wotseguka, ndi wokonzeka kwa wina aliyense kwa nthawi ina iriyonse kwa amene akufuna kubwera mkati ndi kupemphera ndi kufunafuna Ambuye. Kachisi ndi wotseguka ndi kudikira, ndipo tikhala tikukudikirirani inu. Muchiike ngati choncho tidzakhala tikukudikirirani inu mawa masana.

5 Kapena pa nthawi ina iri yonse imene inu mwafuna kuti mulowe mukachisi ndikupemphera, chifukwa, icho ndichokonzeka nthawi zonse. Ndipo ngati chitachitika kuti zitseko zatsekedwa kapena china chake, kungodutsa m'sewu uko m'bale wanga, amene ali wosamalira pano …. Ine ndikuganiza ndi 411. Ine ndikukhulupirira choncho … kapena 811. 811, monga choncho … mwachidule kuchokera kukachisi kuno. 811. Kapena mkazi wake adzakhala ndi mafungulo ngati adzakoke chitseko limodzi ndipo chimatsekeka. Koma amachisiya chotsekula. Mwina cha m'mawa atsekula icho, msonkhano ukatha chimatsekedwa usiku, kupewa ana kuthamangathamangamo, mukudziwa ndi kuswa mawindo ndi zina zotero. Mukudziwa momwe ana amachitira, makamaka mutsiku ili. Choncho timatseka kachisiyu pa chifukwa chimenechi.

Timadana ndi kukhala chitseko chiri chotseka cha kachisi nthawi ina iriyonse. Mwina pamene zina zidzaikidwe tidzapeza izo choncho zidzakhala zosiyana pa nthawi imeneyo, wina atha kukhala m'menemo nthawi zonse kotero kuti anthu atha kubwera kulowa ndi kupemphera, ndi kufuna machiritso, kufuna Mzimu Woyera. Inu amene mulibe

Mzimu Woyera m'moyo mwanu, bwerani pansi, khalani pano. Tangokhalani usiku wonse ngati mukufuna kutero. Tangokhalani mpaka mutaulandira iwo.

6 Kodi ndi ndani amene wachoka pano kanthawi kapitako akuimba, "Mulungu yense pa ine ndi Mulungu pena paliponse"? Ndinaganiza ngati Mkwatulo unali utabwera. Ndinayang'ana mozungulira uko ndi kuona ngati wina aliyense anali alipo. Zinali zodabwitsa zedi. Ndikuyamikira zimenezo. Tikanatha kuimirira pang'ono kwa nthawi imeneyo. Inde, bwana. Ndangolowa m'nthawi yake kuti ndimve zimenezo. Ndaphonya mayimbidwe onse abwino m'misonkhano imeneyi chifukwa ndinaganiza mwina kuti ….

O, ndango … choncho wotangwanika. Mukudziwa inu m'mene ziriri. Anthu abwera kudzera pa denge, pa sitima, pa … inu simungathe kudziwa izi, mukuona, chifukwa chikungobwera kudzera pa lamya. Uyenera kupita kwa iwo, kukumana nawo, ndikuwapempherera iwo, pena paliponse. Chikungopita mosalekeza. Ndipo kuyesa kuwerenganso, chimapangitsa icho kavuto. Koma ife timakhala okondwa nthawi zonse kukumana ndi anthu ndi kuchita zomwe tingathe kuchita kwa iwo, chifukwa ndi zathu …. Ife ndi antchito wamba a Ambuye Yesu Khristu kwa anthu Ake mutsiku lino. Timakonda kuchita

mochuluka kuposa m'mene ife timachitira, koma sitingathe kutero.

7 Mtumiki anabwera mothamanga m'mawawu, atatheratu ndi manjenje basi kungoswekeratu, kungosala zidutswa. M'bale wabwino. Ndipo chifukwa izo iye anali … iye anangogwira ntchito kwambiri. Anayamba kuyimirira. Kamsungwana kake kakang'ono kanali kataima muchipinda. Iye [sungwanayo] anayamba kuzungulira. Anali ndi kachovala kake kogonera kakang'ono kofiira. Anati chinthu chomaliza chomwe iye akukumbukira kanali kadontho kakang'ono kakupita mozungulira, mozungulira, mozungulira, mozungulira, monga choncho. Kupita kunja mwaona. Ndipo choncho iwo anathamanga naye apo.

Choncho yangokhala ntchito yochuluka, inu mukuona. Kumbukirani inu, inu ndi chithupithupi. Ndipo tikuganiza kuti chipsinjo chonse chaikidwa pa ife koma mukudziwa, Mulungu ali ndi antchito Ake pena paliponse kuti akasamale zina za izo, ndipo choncho ife tikungochita mwabwinoko m'mene ife tingachitire. Koma m'tumiki wokondedwa

kuyesa kuchita zonse zimene angakwanitse m'masiku omaliza kwa Ambuye wake, ine ndikutsimikiza …. Ndipo Ambuye anamuombola iye, kumubweretsa iye mbuyo monga momwe iye amakhalira, chabwino, ndi kupita panjira yake akukondwera.

8 O, chinthu chachikulu chachitika lero. Ine sindikufuna kuputidwa pa zinthu zimenezo, koma …. Inu mukudziwa, ine ndinamuuza mkazi wanga, ine ndinati, “Tsopano pakhala munthu wina ali kubwera apo. Iye akhala mwamuna, wamfupi, wokulupala, watsitsi loderako ndi maso oderako. Iye adzawerenga chizindikiro chimenecho ndikuyamba …. koma inu mumuitane iye, mwaona,” ine ndinanena, “Chifukwa Ambuye ali ndi Uthenga kwa iye.” Ine ndinadzuka kuti nditsekule Baibulo, ndipo ine ndinanena, “ine ndiika zinthu zonse izi m'kati muno, choncho mukuona zimenezo ndi ndendende zomwe Ambuye amafuna kuti iye adzichita.”

9 Zaka zisanu ndi zitatu zapitazo, mwamuna wa chi Polish wochokera ku Poland, wokulira ku Poland, pa msonkhano anabwera patsogolo. Ndipo iwo ananena kuti … kapena Mzimu Woyera unamuyang'ana iye, kumuuza iye, kunena kuti, “Mwangosokonezeka.” Ndi chomwe … iye anaganiza kuti ine ndinanena ichi, koma Mzimu Woyera ndi umene unanena ichi. Unakhala ndi iye nthawi yonse, ndipo komaliza unamukankhira iye kuchokera ku Mzinda wa Kansas ku chinyumba usiku watha. Ndipo iye anasokonezekadi pamene iye anamva zokhudza ubatizo wa m'madzi. Iye anapita Kumalo ake ogona ndipo Mzimu Woyera unanena kuti, “Dzuka tsopano, ndipo upite kumtunda uko.”

Munthu winawake anafuna kuti abwere limodzi ndi iye, koma iye anakana izo, chifukwa m'masomphenya iye anabwera pa iye yekha, mwaona. Ndi choncho … ndipo, yowoneka ngati njonda, kudzawerenga chizindikiro, kuyamba kubwerera pa mbuyo. Ndipo mkazi wanga anamuitana iye, ndipo ndinapita ku chitseko. Ine ndinanena, “Ndi ameneyo. Muloleni iye abwere kuno.”

Iye ananena, “Kodi ine ndiyenera kutani?” Iye ataona anati, “Aa, ndachiona.”

Ine ndinati, “Ine ndimafuna ndikuwonetseni inu, chonchonso inu mudziwa tsopano, mwaona.” Ine ndinanena, “Ambuye anandiuza ine kuti inu mukubwera. Inu

munamfusa iye ….“ ndinanena, ”Tsopano pano pali Lemba werengani ilo pano musanapitirire.“

10 Chabwino, iye ali pano kuti akabatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu tsopano. Iye ayenera kuti wabwera ali muno tsopano, kwa zonse ine ndikudziwa. Kodi muli pano, M'bale? M'bale, M'bale wa chi Polish? Inde, kumbuyo uko pa ngodya kuno. Kwezani dzanja lanu m'mwamba choncho iwo angathe kukuonani inu. Chabwino.

Inu mukuona, Mzimu Woyera …. izo zimangochitika nthawi zonse. Anthu ambiri amaganiza kuti masomphenya amangobwera pa guwa basi. O, izo sizimayambisa izo. Kodi ndi chiyani ichi, M'bale Leo? Basi pena paliponse, mwaona. Chabwino, awa ndi malo ang'ono a ichi, pano. Awa ndi malo amene zimachitikirako pang'ono. Kunja uko … ndikumene chimapitako tsiku lonse ndi usiku, inu mukuona. Mfunseni mkazi wanga ndi enawo, ndi oyandikana nawo anga kumbuyo uko, M'bale Wood, ndi onse amene ali ozungulira. O kalanga, izi ndi zinthu zazing'ono pano. Ndi zinthu zazikulu zimene zikuchitika kumeneko. Tsopano, ndipo theka sizinafotokozedwepo.

O, ndiri wokondwa kwambiri pa ichi, podziwa kuti Ambuye wathu akubwera posachedwapa, ndipo tikhala ndi iye kwa nthawi za nthawi osati kwa nthawi za nthawi; koma kwa muyaya - kwa muyaya.

11 Tsopano, Ambuye akalora, ndi kukhulupirira ndi la 18, Lamulungu Sabata likudzali. Lamulungu sabata likudzali, la 18. Ine ndinali ndi nkhondo yovuta. Satana anayesetsa kundipatsa ine chimfine chimene ali nacho chimene chikuzungulira kuno. Ine ndangokhala ndi kumachibwezera kwa iye, ndipo iye akuchibweza kwa ine, ndi ine kuchibweza kwa iye. Ndipo choncho ine ndinali ndi kankhondo kakang'ono. Choncho tiyimalizitsa nkhondoyo mwina sabata la mawa.

Ndipo kotero, Ambuye akalora, Lamulungu likudzali, pa 18, ndipo tidzayesa kubweretsa msonkhano

wina kuti tipempherere anthu odwala chifukwa iwo ali …. zinthu zikuchulukira chulukira; ndi zenizeni zoti zaopsa kwambiri tikuyesera kudzisamala m'mene tingathere, ma ora … ma ora onse a usiku, ndi zina zotero … amabwera napita. Choncho, pa 18 tidzakhala ndi nsonkhano wachizolowezi wa machiritso, ndipo ngati muli ndi ena

mwa okondedwa anu amene akufuna kuti apemphereredwe, chabwino, inu muwabweretse iwo apa kapena muwabweretse iwo mkati pa nthawi imeneyo.

12 Tsopano, pali ambiri achibale a ku Jeffersonville amandiuza ine, amanena kuti anabwera munthawi yake kufika kuno pafupifupi 5 koloko. Akunena kuti panalibe ngakhale malo a magalimoto awo, kapena mipando. Choncho iwo … ine ndinanena, “Chabwino, awa ndi abale athu odzatichezera kuchokera kwinakulikonse. Anthu, atumiki ambiri,” ine ndinanena, “iwo akhazikika pa kuphunzitsa uku.”

Ndipo ife tikungoyesera kuti tingokhuza mituyo; ndipo kenako chamtsogolo pang'ono, chifukwa, tikhala nazo m'mabuku kutero kuti inu mutha kuwerenga izo. Ndipo pazakhala zina zochepa zoonjezera pa izo, chifukwa usiku …. Inu munazindikira mausiku angapo apitawo, ine ndakhala ndikuyesa kuti ndisunge mawu, inu mukuona, chifukwa cha chimake chachikulu icho, ndi zomwe ine ndikufuna kuti ndione - kumeneko kumene vumbulutso la Khristu kupangidwa mu m'badwo uno, mwaona, ndi chimene icho chiri.

13 Ndipo tsopano, tisanayambe kuwerenga Malemba…. Ndipo ine ndikudziwa mawa pokhala tsiku lalikulu la malonda pamene tonse tipite kukagula katundu wogwiritsa ntchito pakhomo wa Loweruka usiku; ndipo tikuyenera kuzipeza izo Loweruka masana kapena Loweruka m'mawa, chimodzi, kotero kuti titha kukhala omasuka Loweruka usiku kuti tibwere kukachisi. Kotero kuti tiyesetse kukutululutsani mofulumira usiku uno kuti inu musatope kwambiri kuti mawa mudzapeze chinachirichonse; ndipo tidzabwerera ku msonkhano wa masana ndi abale pompano ndi ma tepi, ndiponso kwa mawa usiku. Tsopano, tingathe kungoimirira kwa kanthawi kwa pemphero ngati inu mungatero?

Ine ndikudabwa, ife tisanapemphere, ngati pali wina pano ali ndi chopempha chapadera kwa pemphero? Ngati inu mungalole icho chidziwike pakukweza dzanja, Mulungu amaona. Tsopano inu mukuona ngati ife tiri mu dziko la kusowa kapena ayi, abale. Ine ndikuganiza pafupifupi anthu makumi asanu ndi anayi ndi zisanu kapena makumi asanu ndi anayi ndi zisanu ndi zitatu pa zana aanthu osonkhana anayimika manja awo ndiyeno …. Tsopano, kumbukirani inu simungathe kusuntha konse popanda Mulungu

kudziwa izo, mwaona. Iye amadziwa malingaliro anu. Iye amadziwa chomwe inu mumafunsacho. Tiyeni tiweramitse mitu yathu.

14 Wokondedwa Atate a Kumwamba, ife tikusendeza chifupi ndi Chiyero Chanu usiku uno, ku M'pando Wanu wachifumu, kudzera mumalonjezano Anu amene Inu munanena kuti Inu mudzamva; ngati ife tikanakhulupirira mukanatipatsa ife chimene ife tinapempha. Ndipo ife tikuvomereza zolakwa zathu zonse.

Ife tazindikira, Ambuye, kuti ife sitiri oyenera kwa madalitso Anu ena aliwonse. Ife sitiri oyenera. Ife tonse sitiri oyenera. Ndipo ife sitikubwera ngati ife ndife oyenera ndikuti tachita chinthu chinachake chachikulu. O, Atate, tikayang'ana pa Gologota, chimene chimachotsa ukulu wonse kwa ife. Ife sitikudziwa kanthu kena kalikonse pano koma Khristu ndi Iye opachikidwa.

Ndipo pamene ife tiona kuti Iye anauka pa tsiku lachitatu molingana ndi Malemba kwa kulungamitsidwa kwathu, kubwereranso m'masiku makumi anayi m'mtsogolo m'maonekedwe a Mzimu Woyera, kukhala ndi ife mpaka kuoneka kwake m'mitambo ku nthawi yotsiriza …. Ndipo ife tikuona nthawi yotsirizayo ikuyandikira ndithu mofulumira tsopano. Ndipo ndife anthu okondwa kwambiri, Ambuye, chifukwa chakuti mwatipatsa ife mwayi waukuluwu.

15 Ine ndiri woyamika, Atate, kuti gulu lomvetsera ili limakhala pansi ndi mitima yoweramitsidwa, ndi kumvetsera mwachete. Ndipo tsopano, Ambuye, ine ndikupemphera kuti Inu muyeretse milomo yanga usiku uno, ndi usiku wina uliwonse, ndi nthawi ina iriyonse imene ndidzibwera pa guwa Lanu kuti ndiyankhule kwa anthu Anu, chifukwa, Ambuye, musalore ine kuyankhula chinachake cholakwika.

Inu mukadali ndi mphamvu yotseka makamwa monga Inu munachitira mu dzenje la mikango ndi Daniel. Ndipo ngati ine ndingayankhule n'komwe chinachake chimene sichinali cholingana ndi chifuniro Chanu, tsekani kamwa yanga, Ambuye, kuti ine ndisayankhule izo. Muwadutsitse malingaliro anga. Ndiikeni ine pamalo abwino, Ambuye, pamene ine ndisayankhule kanthu kena koma choonandi. Chifukwa ine ndikuzindikira kuti

mu tsiku lalikulu ilo anthu awa adzakhala akudikirira kumeneko pa… kudikirira molingana ndi utumiki umene ndalalikira kwa iwo.

Ngati inu mubwera kudzatenga zina mwa nyenyezi Yanu ndi Angelo Anu, atumiki Anu, akapolo Anu, iwo adzafunsidwa koyamba molingana ndi ma uthenga awa amene ife takhala tikulalikira pano. Inu mudzawafunsa kuti ayankhepo - akapolo anu.

Tsopano, Atate, ine ndikupemphera kuti Inu mulole Mzimu Woyera uyankhule osati munthu. Dulani mitima yathu kuti timumve Iye. Ine ndidzakhala ndi kumvetsera, Atate. Ndikupemphera kuti Inu muchiza odwala ndi osautsika. Zonse zomwe anthu akuzisowa, kwina kulikonse, lorani chisomo ndi chifundo chanu chikhale ndi iwo. Perekani chopempha china chirichonse chimene chinapangidwa kudziwika usiku uno ndi dzanja lokwezedwa m'mwamba.

Kunja kudutsa m'dziko pamene ena ambiri akuvutika, ngakhale iwo amene mipango iyi ikuimirira, ndi zopempha izi zaikidwa pansi m'manja mwanga kuno, lorani, Mzimu Woyera ayankhe, Atate, ndikuchiritsa odwala. Lankhulani kwa ife tsopano kudzera mu Mawu Anu olembedwa, mwa Mzimu Woyera, ife tikupempha mu Dzina la Yesu. Ameni. Khalani pansi.

16 (Tsopano usiku uno kwafunda pang'ono mukachisimu)

M'badwo waukulu wa Mpingo wa Laodikaya ukubwera, ndipo usiku uno ife tikuyandikira ku m'badwo wina wa mpingo waukulu, umene udzakhala m'badwo wa mpingo wachisanu. Ife tatenga m'badwo wampingo woyamba, umene unali wa Aefeso. Ine mwina ndiwerenge izi kachiwirinso poyambirira. Izo zonse zalembedwa, ndipo choncho ine ndikufuna ndiwerengenso izo kwa inu amene mukufuna kuti mutsimikizire m'mapepala anu.

17 M'badwo wa mpingo woyamba unali M'badwo wa Mpingo wa Aefeso, kuyambira A.D. 55 mpaka 170, Paulo pokhala nyenyezi, ndipo unali m'badwo wa mpingo woyamba. “Ntchito zopanda chikondi;” linali dandaulo la Mulungu. Mphotho yake unali Mtengo wa Moyo

M'badwo wa mpingo wachiwiri unali 170 mpaka 312 Irenaeus kukhala mthenga wa tsiku limeneli. Ndipo dandaulo linali kuzunza … zinali zisautso, ndi mpingo wozunzidwa, mphotho, korona wa moyo.

M'bawo wa mpingo wa chitatu unali Pergamo, Martin Woyera kukhala mthenga ku mpingo umenewo. M'badwo wa Mpingowo unachokera mu 312 mpaka 606. Chodandaula chinali chiphunzitso chabodza, Satana akuika maziko a ulamuliro kwa Papa, chikwati cha Mpingo ndi boma limodzi. Mphotho yake inali manna obisika ndi mwala woyera.

Ndipo M'badwo wa Mpingo wa chinayi unali wa Thiyatira, Columba kukhala M'ngelo wa M'badwo wa Mpingo umenewo, m'thenga - 606 mpaka 1520. Ndipo M'badwo wa mpingo anali Papa akunyenga, Mibadwo ya M'dima. Usiku watha, inu mukudziwa, Mibadwo ya M'dima. Ndipo mphotho yake inali mphamvu kulamulira mafuko; ndi nyenyezi ya m'mawa kwa M'ngelo.

18 Tsopano, usiku uno, ife tikuyambira pa m'badwo wa mpingo wachisanu, umene uli Mpingo wa Sarde, Sa - r - d - e, Sarde. Ndipo mthenga ku m'badwo wa mpingo umenewu anali Martin Luther - wakhala wodziwika kwambiri kwa ophunzira Baibulo kapena mphunzitsi, kapena osonkhana, kani, lero. Ndipo m'badwo wa mpingo umenewo unayamba mu 1520 ndipo unatha 1750. 1520 mpaka 1750, ndi m'badwo umene timautchula kuti ndi m'badwo wa kukonzanso. Ndipo chodandaula chinali: kugwiritsa ntchito dzina lawo lomwe; ndipo mphotho ya ochepa otsalira omwe anatsala kunali kuyenda pamaso pake atavala zoyera, ndi maina awo m'Bukhu la Moyo la Mwanawankhosa. Ambuye atidalitse ife pamene tikuyamba tsopano.

Tsopano ife tikuyamba pa ndime yoyamba yamutu wa chitatu, ya m'badwo wa mpingo uwu, uthenga wa ku Sarde, nyengo ya kukonzanso. Ochepa okhulupirika otsalira omwe anatsala, basi pafupifupi kuti athe.

19 Tsopano kwa ena ainu ongobwera kumene, akhoza kuyankhula pa ichi apa, kuti … kotero kuti inu musatsalire pambuyo mu izi…. (izi pena ndi zosalongosoledwa bwino, ndipo nthawi zina ife tifika poti tikayike mauthenga athu kunja pa …. Kuchijambula icho, kubwera masana ndi kuzachikonza bwino. Mwina tichita izi Lamulungu.)

Tsopano, izi chinachirichonse chikuimirira m'badwo wa mpingo: choyamba, chachiwiri, chachitatu, chachinayi, chachisanu, chachisanu ndi chimodzi, chachisanu ndi chiwiri. Ichi, kuyambira ndi Filadelfeya; ndi ichi pamwamba apa chikuimiririra mphamvu za Chipentekosite, kapena Mpingo umene unali pa Pentekosite. Unali Mpingo waukulu pa chiyambi, koma iwo anayamba mzimu wachipembedzo ukubwera pakati pawo, kuyesa kupanga chipembedzo mpingo, umene umatchulidwa “ntchito za chi Nikolayi.” (Kodi mukundimva ine kumbuyoko? Chabwino.) Ntchito za chi Nikolayi. Tsopano ichi chinali chisanakhale chiphunzitso.

Ndipo tsopano ife tinatenga Mawu ndi kuwasanthula - kodi ntchitozo zinali chiyani? Kodi chi Nikolayi chinali chiyani? Ilo ndi dzina la chirendo kwa ife - chi Nikolayi. Kotero ine ndinatenga chi Herene ndi kuchisanthula icho. Ndipo Niko amatanthauza kugonjetsa, kapena kulaka, kapena kulanda ulamuliro wa chinachake. Chi Nikolayi “layi” ndi mpingo osonkhana. Chi Nikolayi: ntchito imene imayesa kulanda ulamuliro wa mpingo, ndi kuika madalitso onse …. Ndipo m'modzi yekhayo woti adziwerenga Baibulo, m'modzi yekhayo woti adzipereka kutanthauzira, ayenera kukhala bishop, kapena wina wamkulu kwambiri wotsogolera pa mpingo.

20 Ndipo ife tikupeza mu M'badwo wa Mpingo wa chiwiri, chinayamba kudzikakamizira kunja. (Ichi chidakali Chipentekosite ndipo ichi ndi Chipembedzo, “C.”) Tsopano, mu m'badwo wa mpingo wachitatu, Pergamo, Pentekosite anali pafupifupi kukanikizidwira kunja. Koma chiphunzitso cha chipembedzo, icho chinabwera kuchokera mu ntchito apa njira yonse m'mpaka ku chiphunzitso apa. Ndipo iwo ndithu anamanga banja apa. Iwo akwatiwa… gulu ili apa limene linagonjetsa magulu a Chipentekosite.

Tsopano m'mene ine ndikunenera izo, abale iyi ndi mfundo yoona. Izi ndi molinga ndi zolembedwa zoyera za mbiri yakale, mabuku aku Necene Council, bukhu la Foxes la nkhani za anthu ophedwera, ndi zonse zolembedwa za kale zikuluzikulu. Ine ndiri ndi zina mwa zolemba zakale kwambiri zomwe zingakhalepo, ndipo wina aliyense ….

Ine ndikunena izi ndi osati…. Osati kunena kuti ine ndine wa Pentekosite. Izo sizitanthauza …. Pamene ine ndinena kuti Pentekosite izo sizikutanthauza bungwe ili la

tsiku ili limene ife tiri kukhalamo. Izo basi ndi ndizolakwitsa ngati ena onseo. Koma ine ndikutanthauza Pentekosite yeniyeni, Mzimu weni weni wa Mulungu ndi chiphunzitso chapachiyambi, ndi madalitso a pachiyambi, ndi maina a apa chiyambi, ndi china chirichonse ndendende m'mene chinayambira pa chiyambi, mofanana m'mene icho chinadutsira mu Baibulo,

21 Tsopano, kenako pamene ife tibwera ku m'badwo umenewu, inu mukuona mtunda omwe chi Pentekosite chadutsa? (Kodi inu mukutha kuona bwino ichi m'buyomo? Inu mukuchirumikiza bwino kumbuyoko? Chabwino.) Tsopano, pano kubwera usiku watha m'badwo waukulu umene ife tirimo pano, Konsitantini. Konsitantini. K - o - n - s, Ine ndichiiika icho. Iye pokhala wachikunja, anawafunsa a Khristu apa amene anali ndi chiphunzitso cha chi Nikolayi - ngati iwo akanapemphera kuti iye akanati apambane nkhondo ina yake, chabwino, iye akanadzakhala M'khristu. Nthawi imeneyo pamene iye anali ku nkhondo, iye analota loto kuti iye akanatha… ndi mtanda woyera umene unaikidwa pa tsogolo pake, ndi kunena, “Pa ichi iwe upambana.” Ndipo izo ndi zolondola. Ndipo iye anadzutsa ankhondo ake ndi kupaka utoto pa zishango zawo mtanda woyera, ndipo pamenepo anali malo obadwirapo kapena kuyamba kwa dongosolo la chi Katolika lero lotchedwa Knights of Columbus.

22 Tsopano, Consitantine, apo pali…. Iwe siungapeze chinthu chimodzi kuchokera mu mbiri yakale za iyeyo ndikukhala wotembenuka. Iye sanali chinthu china koma tambwali wa ndale. Iye anali ndi maganizo m'malingaliro ake obweretsa pamodzi ufumu wake ndi kuupanga kukhala wa mphamvu. Kotero iye, iyemwini, pokhala wachikunja, amapembeza mafano. Ndipo iye anaona kuti chiphunzitso cha chi Nikolayi chinali chitalowerera kufika pa malo, kotero iye anagwiritsa njira yomweyo imene tinayiona usiku watha. Ndipo Yesu analosera izi zaka 304 izo zisanafike pochitika, kuti iye akanadzaphunzitsa chiphunzitso cha Balaam - m'mene Balaam uja ananyengera ana aIsrael, kuwapangitsa iwo kuchita ziwerewere ndi kuperekedwa … kutenga zinthu zoperekedwa ku mafano, kudya zinthu.

Ndipo, ife tikudziwa kuti kudya zinthu izi zoperekedwa ku mafano, chomwe izo zinali kwenikweni kunali kupembedza. Polowa umo, iwo amagwadira pansi mafano, kuikanso mafano mu tchalitchi cha chiKhristu - chimodzimodzi monga Balaam anachita

m'mbuyo umo, anapangitsa aIsraeli kuchita ziwerewere - kupita ku phwando la fano lalikulu ili.

23 Chabwino, Konsitantini anachita chinthu chomwecho ndi kachitidwe kake, ndipo iye anapanga mpingo.

Iye anapereka zambiri ku Nicene Council. Ndipo iye apanga nyumba zambiri zazikulu zomwe iye anali nazo, ndipo anazisandulitsa izi kukhala matchalichi. Ndipo tsopano iye anapanga guwa lamwala wonyezimira lalikulu, lokongoletsedwa ndi golide ndi miyala ina yamtengo wapatali. Pamwamba apo iye anaikapo ngati mpando wa chifumu, ndipo iye anapanga munthu m'modzi kukhala mutu, monga … iye amatchulidwa nthawi imeneyo bishop, ndipo iwo anamuika iye pamwamba pa mpando umenewu.

Boniface wachitatu anaikidwa pa mpando. Osati kokha kuti iye ankangoyenda mozungulira ndi zovala ngati m'mene ankachitira anthu wamba, koma iwo anam'pangira iye… minjiro yayikulu yabwino ndi kumuveka iye apo ngati Mulungu, ndi kumuika iye pamwamba apo ndi kumutchula iye Vicar. Vicar, kapena Vicarius Filii Dei. Izi zikutanthauza “m'malo mwa Mwana wa Mulungu.”

24 Tsopano izi ndikwa iye amene ali ndi nzeru. Jambulani, lembani zimenezo: Vicarious Filii Dei. Ndipo pamene iwe ujambula mzere pansi apa, ndi kuonkhetsa ma nambala … ndipo inu mupeza ndendende chimene Mulungu ananena za chilemba cha chirombo: mazana asanu ndi limodzi ndi makumi asanu ndirimodzi ndi mphambu zisanu ndi imodzi [666], mwaona. Vicarious Filii….

Tsopano, ine ndinafikako ku Roma, ndipo ine ndinafika mu Vatikani ndi korona wa patatu - kukhala ndi ulamuliro wa Gahena, kumwamba ndi purigatorio, mwaona ndinaona korona, ndinaona chovala chaunsembe, ndinaziona izo kumeneko. Makamaka, lachinayi masana 3 koloko ndinayenera kuti ndikakumane ndi Papa wotsiriza amene anali kumeneko. Baron Von Blomberg anali ndi … ndipo iye ananena, “Tsopano pamene inu mupita, M'bale Branham, chinthu choyamba inu mukachite ndi kugwada

pansi pa bondo lanu la manja ndi kupsopsona mpheteyo,”

Ine ndinati, “Zimenezo zichoke; zimenezo zichoke ingoiwalani zimenezo.” Ine ndinanena, ine ndipereka zanga…. Ine ndiribe kanthu kena kotsutsana naye mwamuna ameneyu. “Iye….” koma ine ndinanena, “Pali chinthu chimodzi. Ine ndidzamupatsa mwamunayu udindo wake ngati iye ali wolemekezeka, izo ndi zabwino. Bishop, Wamkulu, Dokotala, ndi zina Zotero, ine ndidzakondwa kupereka ulemu kwa mwamunayu. Koma kupembeza munthu? Ine ndimapereka ulemu wanga wogwadira kwa mwamuna m'modzi: Yesu Khristu. Ameneyo ndiye mwamuna yekhayo ine ndingagwade pa maso pake.” Ine ndinanena, “Tangoiwalani zimenezo. Basi zifuteni izo.” Ine sindingazitenge izo.

Ndiyeno, nditabwerera kunyumba ine ndinapeza kunja uko panali wa Chimerika wina wamkulu anachita zimenezo, ndiponso - Teddy Roosevelt. Iye anakana kuchita zimenezo pa chifukwa …. Kodi inu mukukumbukira izo mu mbiri yakale? Kuti iye anakana kuonana ndi Papa chifukwa iye anali kuti akapsopsone mphete yakeyo kapena …. Iwo ali nayonso pa chala chachikulu ka kuphazi, inu mukudziwa. Kotero … oh, ayi. Ayi, izo kunja uko. Kotero ndiye.

25 Mchifukwa icho, mu …. Tsopano, monga Balaam …. Ndipo ife tinapeza usiku watha, kupitirira ….

Tsopano, (pano choyamba, ife tisanachoke pano), iwo anaulimbitsa mpingo uwu ndi kukwatitsa…. kupeza malingaliro ena a chikunja, mafano a chikunja omwe anali mu Mpingo. Mulungu wa Jupiter, Mulungu wa dzuwa, Mulungu wa Mars, Mulungu wa Venus ndi yonse mafano onsewo a milungu …. ndipo iye anatenga onsewo kuchokera mu Mipingo ya chikunja, ndi kuikapo Paulo, Petro, Namwali Maria, onsewo. Ndipo ananena, “apa pali Vicar wanu, chifukwa Yesu anamuuza Petro, 'ine ndikupatsa iwe mafungulo,' ndipo iye ndi wolowa m'malo wa utumwi.” Icho chidakali chiphunzitso cha Katolika mpakana lero. Ndipo iwo aika apo mafano, ndipo kodi iwo anachita chiyani? Anabweretsa kupembedza mafano mu chi Khristu. Chotchedwa chi Khristu; osati chi Khristu chenicheni, chifukwa a Chipentekosite ochepa….

26 Tsopano kumbukirani, ine sindinanene a Baptist, Methodist, Presbateria. Iwo onse ali momwemo. Koma gulu lenileni loona la Mulungu linali la Pentekosite. Linali, liri ndipo

lidzakhala liripobe. Apa ndi pamene Mpingo unayamba - pomwepa ndi mphamvu za chi Pentekosite. Tsopano, inu mukunena, “Izi ndi zoona, M'bale Branham?”

Ine ndikufunsani inu kuti mutenge mbiri zakale ndi kuyang'ana pansi kupyolera mu nzere wa nthawi mpaka pano, ndi kupeza ngati wina aliyense wa iwo ndi ana enieni a Mulungu sanagwiritse pa madalitso a chi Pentekosite. Anayankhula m'malirime, kutanthauzira malirime, anali ndi zizindikiro ndi zodabwitsa, kubatizidwa mu dzina la Yesu Khristu. Ndi chinachirichonse chimene atumwi anachita, iwo anachitanso, kudutsa monsemu.

Icho ndi chifukwa chimene umo, kuwerenga mbiri yakale, ine ndinatenga Paulo, ndi Irenaeus, ndi kufika kwa Martin Woyera, Kolamba. Wina aliyense wa amuna amenewo, kutsika pansi mpaka kufika mu m'badwo uno, anali ndi zizindikiro ndi zodabwitsa.

27 Chabwino. Iye amati za - za chinkuza mawu chinali ndi pang'ono … kodi izo ziriko bwino? Chabwino. Ayi, iwo anagwedeza mitu yawo; iwo sangathe kumva icho nkomwe, Bill. Chabwino. Kodi inu mungathe … ndi choncho … tsopano, kodi inu mungathe kundimva ine tsopano? Tsopano, bwanji pamenepa? Izo ziri bwinoko? Kodi izo … wina aliyense akunena, “Chabwino, Bone.” Imeneyo ndi malikisi imodzi kuchotsedwa kwa iwe. Chabwino, ziribwino.

28 Tsopano, m'badwo uwu pano, pamene iye anapanga chinthu chachikulu ichi, ndi kumuika mwamuna uyu pano ngati bishop wapenapaliponse pamwamba pa mipingo yonse, kuwapatsa iwo ndarama zambiri ndi zina; ndi kuwalonjeza iwo… anayanjanitsa mpingo ndi boma pamodzi, ndi kulora mpingo kumalamulira boma…. kumupanga iye kukhala mwamuna wamkulu. Kotero apo ziri ndendende….

Chimene Konsitantini anachita ndi chinthu chomwecho chimene ife tikuchipedza apa mu Mpingo wina uwu umene … chimene Mulungu ananena, kuti m'masiku a Eliya kuti iwo analola mkazi uja Yezebeli kugonjetsa ana Ake. Zimenezo zinachitika mu M'badwo wa M'dima. Ndipo yang'anani apa pamene Pentekosite ali tsopano. Kalanga ine, Kalanga ine! Kungouthimitsa iwo. Ndipo kwa pafupifupi zaka chikwi chimodzi, kuchokera

mpaka 1,500, chabwino … imeneyo ndi 606 kufika 530, 520, ndi manambala olondola, koma pa zaka chikwi, iwo adza… kuzunzidwa kwa mwazi - Werengani mbiri yakale.

29 Tsopano, a Katolika akuuzani inu kuti mpingo wa chi Khristu… iwo anali Mpingo wa chi Khristu. Iwo ali mpingo wa chi Khristu wa chipembedzo. Koma Pentekosite woona anakankhiridwa kunja, kuphedwa, kunyongedwa, ndi kuperekedwa ku imfa ndi mapapa ndi mabishopu, ndi ena otero - mwamagazi monga momwe izo zikanakhalira.

Tsopano tsiku lina izo ndi zomwe zidzanditengere ine moyo wanga, mukuona, kuyankhula zimenezo.

Koma icho ndi chinthu chimodzi chotsimikizika, ine ndikudziwa njira imene ine ndikulunjika. Ukungopitirira kukha magazi. Koma ilo likufuka ora tsopano pamene inu muona, malingana ndi zomwe zikuchitika mu fuko, kuti izo sizitenga nthawi yayitali. Musayerekeze kubwerera m'mbuyo pa icho. Icho ndi choonadi. Inu khalani nachobe. Sakanizani magazi anu monga iwo m'tsiku lija.

30 Tsopano, umu inu mukuona chomwe chinachitika. Kenako umu

chiphunzitso cha Yezebeli chinalowamo. Yezebeli anali mkazi, wachikunja, amene …. Ahabu anachita chinthu chomwecho chimene Konsitantini anachita - anakwatira mkazi uyu ndi cholinga kuti alimbitse ufumu wake, ndipo anabweretsa za mafano mu Israeli - basi ndendende monga Konsitantini anachita kumbuyo uko.Ndipo chi Pentekosite chinali pafupifupi kutha chonse. Tsopano Mulungu anadzutsa Martin Luther.

Ine ndikufuna inu muzindikire m'mene icho chapitira kunja kuno ndi pafupifupi kusoweratu chonse, ndipo pang'ono ndi pang'ono chikuyamba apa ndipo chikuyenda kufika apa. Ndipo ine ndinayika chizindikiro pamenepo, chifukwa ilo ndi phunziro lalikulu la Lamulungu usiku, Ambuye akalora.

31 Ine ndikukhulupirira ife takhala ngati takodwa tsopano apa pamene ife tiri.

Tsopano umu apa ndi M'badwo wa M'dima, cha apa, kuyambira 1500 … kuchokera 606 mpaka 1520. Cha umu apa. Ine ndiyika izi apa kuti inu mudzi… 606 mpaka 1520. Umenewo ndi M'badwo wa M'dima, Mpingo uwu apa. M'badwo wa M'dima. Tsopano,

Mpingo uwu umene ife tikufikako pa iwo tsopano ndi mpingo wa Luteran. Tsopano, pafupifupi aliyense kumbuyo uko, anthu amenewo anafa uko mu …. Amuna awa ngati Irenaeus, ndi Martin, ndi Columba, ndi iwo anazimirira.

Ndipo tsopano inu mutenge wina aliyense amene akufuna, fufuzani kumbuyo uko m'mbiri ya kale ina iriyonse yomwe inu mukufuna, ngati iyo ili mbiri yakale yovomerezeka, ndipo pamene iwo akukuzani inu kuti Patrick Woyera anali wa Katolika, iwo sakudziwa chimene iwo akuyankhula. Patrick Woyera anautsutsa mpingo wa Katolika ndipo sanapitepo ku Rome, ndipo molimba anakana chiphunzitso chawo. Ndendende kulondola. Mupite ku mpoto kwa Ireland lero ndipo inu mudzaona chinthu chomwecho. Patrick Woyera anali munthu wa Mulungu. Koma Patrick Woyera, pamene zinanenedwa m'menemo kuti iye anathamangitsa njoka zonse kuchoka mu Ireland imeneyo inali nthano.

32 Ndi angati a inu anawerenga ndi kumva zokhudza William Tell kuwombera apulo kuchokera pa mutu wa m'nyamata wake? Imeneyo ndi nthano ya Katolika, panali cholembedwa cha izo choncho. Ine ndinali pomwepo pamene ichi chinayenera kuti chinachitika. Ichi chinalembedwa apo, “Nthano - si chincho,” mu Switzerland.

Billy ndi Ine tinakhala pamenepo pa mbali pa Nyanja ya Lucerne pamene iye anachita icho. Iye anawombera munthu, izo ndi zoona - koma osati apulo kuchokera pa mutu wa mnyamata wake. Izo ndi nthano chabe, zikhulupiriro, ndi zinthu. Icho sichinali choncho. Iwo alibe zolembedwa za ichi apo pamene ichi chinachitikira, kapena chinachake kuti iwo anachita ichi. Ndipo ichi makamaka chilongosola ichi kumeneko ndi kunena chomwe icho chinali. Tsopano, koma mu izi… ndipo palibe mbiri yakale imene ikunena kuti iye anachita ichi.

33 Choncho tsopano mkati umu, mu m'badwo wa mpingo, umu ndi momwe chinali pafupifupi kuzirala, kupitiratu osaonekanso. Ndipo mu m'badwo wina uwu ukubwera m'badwo wokonzanso. Tsopano, zinthu izi apa, patatha pafupifupi zaka chikwi za kudetsedwa ndi mdima, ndi kuzirala ndi zina ngati zimenezo, Mpingo unakhala ngati unataya kuona kwa Irenaeus. Iye anali mwamuna wamkulu, mwamuna wa umulungu.

Koteronso anali mazana ambiri a iwo woyera mtima awo amtengo wapatali amene anapereka mwazi wa moyo wao basi mwa ulere ataima mu bwalo lazamasewera limenelo monga akanathera - pa chifukwa cha Khristu, chifukwa cha ubatizo mu Dzina la Yesu Khristu, chifukwa cha kuyankhula m'malirime, chiukitsiro cha Yesu Khristu, kukhalapo m'moyo ndi kupezeka kwake kwa umulungu pamenepo - pamene anthu ozitchulira okha Akhristu anali akuwazunza iwo izo ndi zolondola. Izo ndi ndendende.

34 Oh, ichi ndi chikhamu cha ziwanda cha ku Gahena, kuyenera ine sindikudziwa chiyani.

Kubwera apo monga choncho, ndi kudziika okha, ndi kudzipanga okha… “Amadzitcha yekha m'neneri wa mkazi,” wotanthauzira Mawu waumulungu. Palibe wina aliyense akudziwa ichi koma iwo. “Amadzitcha yekha ….” Koma iye ndi wa bodza, mwaona. Koma mu nthawi yomweyo… Ali, m'ngelo Wake pamenepo ndi choonadi. Choonadi nthawi zonse chidzapita kubwerera kwa ichi, mwaona. Nthawizonse kupita kubwerera ku chiyambi chifukwa Mulungu samasintha kuchokera pa izo.

Tsopano, ndipo ife tinazipezanso mu usiku watha (ife tisanachoke ku ichi, kuti ichi chidzakhazikike mu mtima mwanu), osati anachita kokha …. Mu choimira, Yezebeli, iye anali ndi mwana ananena izi za wa

mkazi. Mukukumbukira zimenezo? Ndipo Chibvumbulutso 13 anati Mpingo uwu wa chinyengo, Rome, unali ndi ana akazi. Iye anali mayi wa timahule. Kodi uko ndi kulondola? Yezebeli anali naye mwana wa mkazi, ndipo ndi chiyani chimene Yezebeli anachita ndi mwana wake wa mkazi? Mwaona, zinthu zonse izo, zoimira ndi mithunzi? Yezebeli anaonetsetsa kuti mwana wake wa mkazi akwatiwe ndi Yehoram, yemwe anali mwana wa mwamuna wa Yehoshafati mu Yudeya.

35 Israeli anali wogawanika pa nthawi imeneyi, ngati chonchi apa pali Yerusalemu apa, ndi pano pali Yudeya apa. Chabwino, Ahab anali apa, ndi Yehoramu anali apa. Chabwino.

Yezebeli anali atagonjetsa ichi, Israeli yense anatenga mafano nthawi imeneyo - onse koma Eliya ndi gulu laling'ono lokhulupirika lija. Chabwino. Tsopano, uko ku mbali iyi kunali Yehoramu ku Yuda. Ndipo pamene mkaziyo anakhala ndi mwana wa Ahab, iye

anamutenga msungwanayi ndi kumukwatitsa kwa mwana wa mwamuna wa Yehoramu… kapena kwa mwana wa mwamuna wa Yehosafati, yemwe anali Yehoramu, ndi kubweretsa za mafano mu Yuda, ndi kuika maguwa a chikunja mu Yerusalemu.

Izo ndi ndendende chimene mpingo wa Katolika unachita. Iwo unatambasula chiphunzitso chake cha chipembedzo ndi zina zotero, ndi kudula Mzimu Woyera kuuchotsa mu mpingo apa ndi mwana wake wa mkazi - a Luteran, Methodist, Baptisti, Pentekostal, ndi zina zotero. Izo ndi ndendende zomwe iwo wachita. Baibulo linanena kuti iye ndi mayi wa timahule. Tsopano inu tangoyang'anani kudutsa Malemba. Ngati inu mukuona chinachake chamtundu wina, chosiyana M'malemba, ndi mbiri yakale ikulunjika ndendende pa zomwezo, inu mubwere kwa ine ngati njonda, mwaona. Izo ndi zoona. Izo palibe.

36 Zipembedzo izi ndi ziphe zoyipa kwambiri zomwe ife sitimakhalepo nazo mumpatuko - kuyesa kumupanga munthu kuti adziramulira mpingo, fano lina longa lomwe linakhala pa mpando wachifumu. Bishopu wamkulu, woyang'anira wa mkulu wa Pentekosite, “Chabwino, tsopano, ndiroleni ine ndiwone, kodi chiphunzitso chake ndi chiyani? oh, kodi Iye amabatiza mu dzina la Yesu? Iye sangabwere mu ichi. Ayi, bwana, m'bale. Inu musachirole icho.” Ndipo icho chakanidwanso.

“Ine ndikupatsani inu kumvetsa, osati ena mwa inu kupita kumisonkhano kumeneko.” Mukaneni. “Palibe kanthu m'mene inu mukudwalira, khalani kutali. Palibe kanthu chimene Mulungu akuchita, ngati inu simukuyang'ana kudzera m'magalasi athu, bwanji, inu simukuona konse.” Fano kwa chirombo, ndipo fano linali ndi moyo okutha kuyankhula. Izo ndi ndendende kulondola. Ngati inu simukuganiza kuti iye angathe kuyankhula, tangomupondani iye chala apo pang'ono nthawi ina. Inu zedi mudzakhala m'mavuto.

37 Ine ndikukumbukira Tulsa, Oklahoma. Ine ndinali…. oh, ine ndinali ndikulowa mu chisokonezo choopsa kumeneko. Azipembedzo awo akhala akuyendayenda mozungulira kumeneko, ndipo ine ndinakhala mu nyumba tsiku lina ndipo ine ndinaona masomphenya. Ine ndinaona kakang'ono … kamwana ka mphaka kakale, kokongola, kakang'ono, ndipo

iye anali atagona pa pillow wa nsalu za bafuta. Ndipo iye anali kanthu kakang'ono kooneka bwino. Ndipo ine ndinayenda kupita pamenepo. Ndipo ine ndimaopa mphaka.

Ndipo ine ndinapita apo ndipo ndinayamba kumusisita iye motsitsa, ndipo iye anapita “kurr, kurr.” Inu mukudziwa m'mene iwo amachitira, ndi phokosolija lachirendo, inu mukudziwa. Ndipo ine ndimamusisita iye motsitsa, ine ndinati, “Kamwana kamphaka kokongola kakang'ono.” Ndipo iye anati, “ kurr,” basi mwabwino, inu mukudziwa. Ndipo ine ndinayang'ana apo paseri pa pillow wake. apo panalembedwa, “mwana wa mphaka wa Chipentekosite.” Chabwino, ine ndinaganiza, “Tsopano ichi sichachirendo?” ndipo ine ndinanena, “Ichi chiyenera kukhala masomphenya.”

Ndipo chinachake chinanena, “Pokhapokha ngati iwe ukusisita ubweya wake motere, ziribwino. Koma tsopano ngati inu mufuna kuti muona zomwe iye anapangidwira, sisitani iye mobwerera m'mbuyo.”

Kotero pamene ine ndinamusisita iye mobwerera m'mbuyo, maso awo anaturuka kunja, obiriwira, ndipo iye anali nyama yolusa, ataima pamenepo ndi kumalavulira pa ine molimba m'mene iye akanathera, mwaona.

Basi kungomusisita iye mobwerera m'mbuyo pang'ono pokha. Umuuze iye kuti ubatizo wake wa Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera ndi wa m'dierekezi ndi wa mpingo wa Katolika. Penyani zomwe zitizichitike kwa iye. Bweya wake anaimirira m'mwamba. Ine ndinabwerako, ndinanena kwa M'bale Gene ndi iwo umo… oh, M'bale Leo ndi ena, ine ndinanena, “Ine ndikutsimikiza ndinali ndi masomphenya enieni a zipembezo za Chipentekosite.”

38 Tsopano mutu wachitatu, tiyeni poyamba…. Sarde ndi Mpingo wakufa. Iwo ndi wakufa chifukwa iwo unaphedwa pa nthawi imeneyi. Kaulusi kakang'ono ka moyo- ife tipeza mu mphindi zochepa chimene ichi chinali mochepa chabe. Kuchokera pa 1520 kufika 1750 unali M'badwo uwu wa Sarde. Ndipo nyenyezi kapena M'ngelo wa …. Nyenyeziyo inali m'dzanja Lake, amene anali m'ngelo kapena m'thenga wa M'badwo wa Mpingo umenewo. Kodi izo zikumveka bwinobwino? Kuti nyenyezi inali m'ngelo, ndipo m'ngelo ndi

mnthenga ku M'badwo umenewo. Chabwino.

39 Tsopano ife tathana ndi Nicene Council. Mkaziyo anafa m'mbuyo m'menemo ndi onse kubwera mu mphamvu ndi ulemerero, Mpingo ndi boma zinalumukizana. Ndipo kodi wina angathe kukumbukira chimene phunziro linanena usiku watha, chimene anthu ambiri aiwo amaganiza? Zaka chikwi zinali zitayamba, ndi zonse zi… kuyambitsa zaka chikwi Khristu asanabwere. Mwaona? Kubwera kwa Khristu kubweretsa kuyamba kwa zaka chikwi, chinthu choyamba. Ndipo m'masiku amenewo iwo anali nawo…. ngati inu mutatenga mbiri yakale inu mupeza kuti iwo anali ndi a yesu abodza atadzuka apo, ndi zinazirizonse, mwaona.

Ndipo iwo ankaganiza kuti papa anali Yesu, kumutchula iye Vicar, m'malo mwa Mwana wa Mulungu, inde. Wamkulu, woyera, wonga mulungu, atakhala pamenepo.

40 Ndiroreni ine ndikuuzeni inu chinthu china. Baibulo likunena kuti pamene Yesu abwera… kusanafike kubwera kwake padzauka aneneri onyenga, ndipo padzakhala kudzuka kwa a yesu onyenga. Izo ndi zoona, “Taonani, apa.”

Koma lorani ine ndingogwetsera ichi m'mtima wanu. Sipadzakhalanso Yesu ataponda phazi lake padziko la pansi mpaka Mpingo utakwaturidwa ndi kupita. Tsopano mungochiika icho m'malingaliro, chifukwa padzakhala a Khristu onyenga adzaukapo. Koma Yesu adzakhala palibe pano padziko, chifukwa Lipenga likulira ndipo iye sangabwere…. Ife tikumana naye iye m'mlengalenga. Mpingo wapita kale. Ndipo tsopano, pamene Yesu awonekera kudzakhala kubwereranso. Amitundu kupita kukakumana naye m'lengalenga. Kodi ichi silemba? Iwo kupita kukakumana naye m'mlengalenga, ndipo tsopano ife tipita m'mwamba. Ndipo Yesu sadzaika mapazi ake padziko lapansi mpaka Mpingo utakwatulidwa ndi kufika kunyumba, ndipo phwando la chikwati likutha. Ndipo Iye adzabwerera pa mbuyo kudzafuna Ayuda otsalira.

41 Kotero tsopano, izo zinatha, Nicene Council. Mpingo wakhala uli pansi pa ulamuliro wa papa pafupifupi zaka chikwi. Iwo anawapha onse amene samagwirizana ndi iwo. Uko nkulondola. Inu mwina mubwere pansi pa icho kapena inu mumaphedwa, monga Yezebeli anachitira kwa Israeli. Mzimu Woyera unawachokera onse, koma ochepa mu

nthawi ya m'badwo uwu, monga Eliya ndi otsalira a Aisraeli amene sanapindire bondo Balaam.

Ngati inu mukufuna ine kuti ndiwerenge zimenezo m'menemo, izo ndi 1 Mafumu, mutu wa 19 ndipo ndime ya 18, pamene Eliya anayima kumbuyo uko mu mphanga. Ndipo iye ananena, “Ambuye iwo awapha aneneri anu onse. Iwo achita chinthu chinachirichonse ndipo ine ndiri ndekha. Ndipo ndi ine ndekha amene ndapulumuka.” Koma Mulungu anamuuza iye kuti anali ndi mazana angapo naponso amene sanapinde bondo lawo kwa Baala, mwa osonkhana kunja uko.

42 Ndi choncho, Sarde. Tsopano ife tikhala tikuyamba. Liwu lomwelo “Sarde” (ndime yoyamba) …. Liwu loti “Sarde,” muchingerezi limatanthauza, ngati inu mukufuna kuyang'ana ilo apa, limatanthauza “Iye wopulumuka.” Sarde woona anali wopulumukayo. Ndi chimene Sarde amatanthauza. Chabwino, wopulumukayo. Tsopano, mwaona, ndi … iye wopulumukayo. Tsopano ife tikufuna tiyambe pa mayambiriro. Ife tikufuna tiutchule iwo kuti m'badwo wa kukonzanso, ndi chinthu choyenera kwambiri kwa kukonzanso uku, ngati ife tingatchule icho zimenezo, chifukwa ndi …. Kukonzanso kunali opulumutsidwawo amene anachoka ndi kupulumutsidwira kuchokera ku ichi.

43 Tsopano tiyeni titenge ndime yoyamba:

…kwa m'ngelo wa Mpingo wa Sarde Lemba; zinthu izi anena Iye amene ali… Mizimu isanu ndi iwiri ya Mulungu, ndi nyenyezi zisanu ndi ziwiri; ine ndidziwa ntchito zako, kuti iwe uli ndi dzina kuti iwe uli ndi moyo, ndipo uli wakufa.

Tsopano malonje. Tsopano, Mizimu isanu ndi iwiri ili … Mizimu isanu ndi iwiri, ndi nyenyezi zisanu ndi ziwiri. Mizimu inali Angelo amene anapita ku nyenyezi, amene anali a mithenga. Mizimu isanu ndi iwiri. Kasanu ndi kawiri nthawi zosiyana Mzimu Woyera unkadzoza mnthenga, yemwe anali nyenyezi mu tsiku lake. Mzimu ndi wa muyaya. Ndipo nyenyezi inapangidwira pa cholinga choti inyezimiritse kuwala mu mdima uwu wa Mibadwo ya mpingo iyi, pamene nyali ndi nyenyezi zikuimiridwa. M'ngelo, Mzimu, unali umene unapita kwa nyenyezi ndi unanyezimiritsa kuwala kwa Mzimu Woyera kudzera mu nyenyezi iyi ku m'badwo wa Mpingo umenewo omwe….

Inu mutha kudabwa kuti Mizimu isanu ndi iwiri ndi ndani. Ndi a mithenga asanu ndi awiri a mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo, mwaona. Tsopano, nthawi ina iriyonse yomwe nyenyezi ifika, Mzimu Woyera umatsika ndi kudzoza nyenyeziyo, ndipo kumaisunga iyo basi ndendende monga momwe yoyambayo inaliri.

44 Tsopano ndiroleni ine nditsimikizire izo kwa inu. Paulo anati…. ngati inu mukufuna kudziwa kodi ndi mtundu wanji wa nyenyezi iyo inali…. Chifukwa, kumbukirani, Satana, ndi nyenyezinso - nyenyezi yaku

m'mawa. Tsopano zindikirani, Paulo anati …. inu mukukhulupirira iye anali nyenyezi ku Mpingo wa Efeso? Iye anati …. Tsopano, ngati inu mukufuna kudziwa ngati ziri zoona kapena ayi, mu a Galatiya 1:8 Paulo ananena, akuyankhula pamenepo (patapita nthawi zikanadzabwera nkhandwe zolusa ndi zina zotero) iye anati, "Ngati m'ngelo abwera kuchokera kumwamba ndi kuphunzitsa uthenga wabwino wina uliwonse…."

Tsopano iye anadziwa kuti munthu uyu akubwera amene amaoneka ngati m'ngelo, Vicar wamkulu. Iye anati, "Palibe kanthu kuti iye ndi ndani, ngati m'ngelo aliyense, kapena munthu wina aliyense angabwere ndi kuphunzitsa chinthu chinachake kupatula uthenga wabwino uwu ife tauphunzitsa kwa inu, musiyeni iye akhale wotembereredwa." Kodi uko nkulondola?

45 Paulo anali iye amene anawakakamiza iwo kuti abatizidwenso ngati iwo sanabatizidwepo mu Dzina la Yesu Khristu - bwerani ndipo mudzabatizidwenso kachiwiri ndi cholinga choti mulandire Mzimu Woyera. Machitidwe Atumwi 19:5

Iye analinso m'modzi amene anasanjika manja pa wanthu, ndi mphatso, ndi kuika Mpingo mu dongosolo, ndi kugwira ntchito kwa zozizwa, machiritso auzimu, mphatso za malirime, kutanthauzira malirime. Kodi uko nkulondola? Akorinto woyamba ndime ya 12, inu mukuona chimene Paulo ananena. Akorinto woyamba 12, inu mudzazipeza izi. Iye anakhazikitsa mu mpingo … Mulungu anakhazikitsa mu Mpingo mphatso zazikulu izi ndipo Paulo anaziika izo mu dongosolo, ndi kuziika izo mu dongosolo kuti izo zikathe kugwira ntchito ku ulemerero wa Mulungu Paulo ananena zimenezo.

Ndipo ngati munthu wina, ziribe kanthu kuti ndi wa chipembedzo chanji, amene angayesere kukuuzani inu kuti masiku akuyankhula m'malirime, kutanthauzira malirime, machiritso auzimu, ndi zozizwitsa, ndi umboni wa Mzimu Woyera ngati ubatizo … musiyeni iye akhale wotembereredwa. Chifukwa Mzimu womwewo umene pa Paulo udzakhala Mzimu womwewo umene unatumizidwa ku m'badwo wa mpingo wotsatira, womwewo ku m'badwo wa mpingo wotsatira, ndipo womwewo kupitirira mpaka kufika ku mapeto a mibadwo ya Mpingo. Mzimu yemweyo, Mzimu woyera. Kodi inu mukukhulupirira izo?

46 Ngati inu mungazindikire ichi, ichi chinalembedwa apa. Wolemba amadziwa. Yang'anani, Mizimu isanu ndi iwiri. Penyani - "M" wamkulu. Mzimu Woyera. Yekhayo m'modzi wa iwo. Mzimu Woyera omwewo kubwera kasanu ndi kawiri ku mibadwo ya Mipingo isanu ndi iwiri yonse ali ndi kuwala kofanana. Kodi inu mukuchimva ichi tsopano? Mibadwo isanu ndi iwiri, nthawi zisanu ndi ziwiri Mzimu Woyera uwu udzanyamula Uthenga womwewu, umene unalengezedwa themberero kwa wina aliyense amene angasinthe iwo.

Tsopano muone ngati izo zikugwirizana ndi vumbulutso la chinthu chonsechi. Iye ananena, "Aliyense amene ati adzachotse kapena kuwonjezerapo, Ameneyo gawo lake lidzachotedwa mu Bukhu la Moyo." Icho ndi chinthu chonsecho chimene chaphimbidwa pamenepo. Kotero palibe malo a inu ku dumphira kapena kuzikakamiza m'malo ena aliwonse, mwaona, chifukwa izo ziri. Izi ndi zimene Mulungu ananena, ndi zimene Mzimu ananena, ndi zimene mipingo inenena.

Tsopano, ngati inu muyesa kukakamizira mkati chiphunzitso china chirichonse kupatula chimene Paulo anaphunzitsa, ndi kulakwitsa Baibulo ndi lolondola. Moyo wake … Yesu anati, "Ine ndidzachotsa gawo lake mu Bukhu la Moyo."

Tsopano, inu mukunena, "Kodi ndi gawo lanji la Bukhu la Moyo?"

47 Pali anthu ambiri amene maina awo ali M'bukhu la Moyo ntheradi adzalephera. Inu mukudziwa zimenezo, kodi inu simukudziwa? Kodi inu mukumbukira kuphunzitsa kuja usiku wina? Kodi inu munachimvetsa ichi? Ndiroleni ine ndibwereze izo. Sizikumveka bwino nthawi ino. Simukumverera bwino, mwaona.

Yudasi Iskalioti anali mwana wa Satana. Iye anali mdierekezi akuwonetseredwa mu thupi. Baibulo linanena iye anali. Baibulo linanena "Iye anabadwa mwana wa chitayiko." Penyani ichi mwa ka mphindi. [M'bale Branham akulemba pa bolodi la kuda.]

Tsopano, pa ichi anali Yesu. Apa panali mbala ku manja kwake, apa panali wina kumanzere kwake. Tsopano, pamene …. Yesu anali Mwana wa Mulungu. Kodi uko nkulondola?

Tsopano, anthu ena amangoona mitanda itatu, koma inalipo inai. Mitanda inai. Tsopano mtanda kodi ndi chiyani? ndi mtengo. Kodi uko nkulondola? Baibulo linati, "Wotembereredwa iye amene apachikidwa pa mtengo." Iye anapangidwa themberero m'malo mwathu, Iye anapachikidwa pa mtengo. Iwo unali utadulidwira, koma iwo unali mtengo. Kodi uko nkulondola? Pansi pano, mutsindetsinde la Phiri panaima wina. Yudasi anadzipachika yekha mu mtengo wa mkuyu. Kodi uko nkulondola?

Yang'anani, apa pali Mwana wa Mulungu, anachokera kumwamba, kubwereranso kumwamba, kutengana ndi iye pamodzi ndi wochimwa wolapa. Pano pali mwana wa chitayiko, kuchokera ku Gahena, kubwereranso ku Gahena, kutengana ndiye pamodzi "Ngati iwe uli …." Wochimwa wosalapa, mwaona. Wochimwa wosalapa. "Ngati iwe uli Mwana wa Mulungu zipulumutse wekha ndi ifenso."

Winayu anati, “Ife takhala [kulalikira, wolalikira uthenga wabwino uyu] …. Ife tinayenera zimene ife tikuzipeza, koma munthu uyu sanachite kanthu. Ambuye, mundikumbukukire ine pamene inu mufika kuufumu wanu.”

Kodi ameneyo anali yani?

48 Pang'ono pokha (usiku watha, kapena usiku winawo.) Uyu ndi Abele wa Mulungu; pano pali Kaini wa mdierekezi. Monga kaini anapha Abele pa guwa, Yudasi anapha Yesu pa guwa. Uko nkulondola. Utsi basi ukungokwerera kuchokera kumbuyo uko mu Edeni ndi kudzakhazikikanso kuno. Izo ndi ndendende. O, izi ndi za ulemerero, msewu wakale uwo, msewu wakale odalitsidwawo. Basi wodzala ndi ulemerero!

Tsopano. Tsopano ife tikupeza pano (Ine ndikupepesa) kuti Mpingo uwu wa Sarde, kwa m'ngelo …. Iye anati, “Mizimu isanu ndi iwiri …Iye amene ali ndi mizimu isanu ndi iwiri….” “Kwa m'ngelo wa mpingo wa Sarde lemba; zinthu izi anena iye amane ali ndi mizimu isanu ndi iwiri ya Mulungu….”

49 Ndipo tsopano ndi angati amene akudziwa kuti Mulungu ndi Mzimu umodzi? Ntheradi. Mulungu, Mzimu Woyera. Mulungu, Atate Mzimu Woyera, zonse munthu yemweyo, chifukwa Maria anatenga pakati pa Mzimu Woyera. Tsopano, koma Mulungu anagwiritsa ntchito Mzimu Woyera uwu mu kuwala kusanu ndi kuwiri kosiyana kwa ulaliki ku Mpingo, mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo. Kodi inu mukumvetsa ichi? Mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo.

Tsopano, inu mukuti, “Mulungu samachita zimenezo.” O, inde,. Onani, Iye anagwiritsa ntchito mzimu wa Eliya. Ndipo pamene Elisa anapita … Eliya anachoka, Elisa analandira magawo awiri a iwo. Ndipo pamene Elisa anadwala ndi kufa, ndipo unabweranso pa Yohane m'batizi. Chinthu chomwecho. Kumupanga iye kuchita munga Eliya anachita - kukhala mu chipululu, ndi zina zotero. Kodi uko nkulondola? Ndipo analosera kubweranso kachiwiri mu masiku otsiriza, mukuona. Mulungu amagwiritsa ntchito mzimu mopitirira.

50 Ndipo Yesu anadzozedwa ndi Mzimu Woyera, anapita nakachita zabwino. Kodi uko nkulondola? Ndipo Mzimu Woyera yemweyo amene anali pa Yesu, anabweranso kulowa mu Mpingo pa tsiku la Pentekosite; kubweranso kulowa mu m'badwo wotsatira, m'badwo wotsatira, m'badwo wotsatira. Ndi chiyani kodi ichi? Ndi m'modzi Mzimu Woyera mwiniwake. O, kodi inu simukuwona? Mulungu pamwamba pathu mwa Atate, Mulungu nafe mwa Mwana, Mulungu mwa if mwa Mzimu Woyera. Ndi maudindo atatu ndipo osati a mulungu atatu, mwaona. Maudindo atatu awo - Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera - ndi za Dzina limodzi: Yesu Khristu. Chabwino.

51 Tsopano, penyani tsopano pamene ife tikupitirira.

Mizimu isanu ndi iwiri, anena iye amene agwiriza … mu mawu ena, kugwiriza a Mithenga ake - a Mithenga amene adzadzozedwe ndi Mzimu Woyera. Ndi Mzimu Woyera

womwewo umene Paulo, woyambayo, anadzozedwa nao, wachiwiriyo, wachitatu, wachinai, wachisanu, wachisanu ndi chimodzi ndi wa chisanu ndi chiwiri….

Onse amenewo ali mu dzanja Lake la manja, O, kutenga mphamvu zawo ndi kuwala kwawo kuchokera mu dzanja Lake la manja. Tsopano, Iye anakwera m'mwamba. Ndipo Fillipo ananena pamene iya amafa… kapena Stefano anati, “Ine ndikuona kumwamba kutatseguka ndipo Yesu atakhala ku dzanja la manja la Mulungu.” Izo sikutanthauza kuti Mulungu ali ndi dzanja lalikulu la manja ndipo Iye akukhala pa ilo, koma dzanja la manja limatanthauza dzanja la manja la mphamvu ndi ulamuliro.

52 Thupi limene Mulungu analirenga… “Sindidzalola Woyera wanga kuti awone chivundi; ngakhale kusiya moyo wake mu Gahena,” koma kumukweza iye m'mwamba ndi kumukhazikitsa iye, m'malo mwa Mzimu, pa guwa. Penyani pamene iwo awona iye atakhala pa guwa, ndipo anali ndi bukhu mu dzanja lake …. Ndipo palibe munthu pa dziko, kapena pansi pa dziko, kapena kwina kulikonse, yemwe anali ndi kuthekera, kapena kuyenera, ngakhale kuyang'ana pa buku.

Koma Mwana wankhosa, amene anaphedwa kuchokera pa madziko a dziko lapansi (mbuyomo pa chiyambi pamene iye poyamba anaganiza za thupi loomboledwa ili), kubwera ndi kutenga ilo kuchoka mu dzanja la manja mwa iye amene wakhala pa mpando wa chimfumu, ndipo anakhala pansi, Iyemwini. Ndizimenezo. Awo nd Malemba. Izo basi ndi zokongola, mwaona.

53 Tsopano, “Iye amene agonjetsa adzakhala ndi ine pa mpando Wanga, monga ine ndagonjetsa ndipo… ndakhala pansi pa Mpando wa Chifumu wa Atate Wanga.” Mu mawu ena, “Ine ndinatengera mkati mwa thupi Langa Mzimu Woyera. Ndinagonjetsa zinthu zonse za dziko kudzera mu mayesero - mwa Mzimu Woyera - ndikutenga ulamuliro.” Ndipo mwa iye muli chidzalo cha umulungu mu thupi.

“Mphamvu zonse ku mwamba ndi dziko la pansi zaperekedwa m'manja mwanga,” Iye ananena. Mphamvu zonse. Ndipo Mulungu ali wopanda mphamvu ngati Iye ali munthu wina. Pakuti Baibulo linati Yesu anati, pambuyo pa chiukitsiro chake, kuti, “Mphamvu zonse kumwamba ndi dziko lapansi zonse

zinaperekedwa mu dzanja Langa.”

Ndipo Yesu akubwera kuchokera kumwamba ndi zikwi khumi kuchulukitsa zikwi khumi za woyera mtima ake, ndipo Baibulo likunena kuti miyamba inali yopanda kanthu kwa theka la ora. Kodi ali kuti munthu uyu wamkulu, Mulungu, nthawi imeneyo? Mukuona? Iye ali mwa Khristu. Indedi.

54 Ndipo ngati ife tigonjetsa ndi Mzimu Woyera monga Iye anachitira, ife tidzakhala ndi Iye pamene Iye akutenga mpando Wake wa chifumu wa dziko la pansi wa Davide, kukhala ndi kulamulira ndi Iye monga m'mene Iye anachita uko (Ameni!), ndi mphamvu ndi ulamuliro pa zonse za pa dziko la pansi.

Ndipo dziko lapansi likubuma, kudikirira kuwonetseredwa kwa ana a Mulungu kuti awonetseredwe, ana a Mulungu. Chifukwa pambuyo pa zonse, dziko ili sirinapatsidwe kuti Mulungu adzirilamulira. Uko nkulondola. Kodi Mulungu wa dziko la pansi ndi ndani? Munthu. Awo ndi malo a ulamuliro wake. Zonse, chinthu china chirichonse, mu dziko lapansi ziri pansi pa ulamuliro wa munthu. Kudzera mu tchimo iye anagwa; kudzera mu mphamvu ya chiwombolo ya Khristu iye akubwereranso kachiwiri. Izo ndi zolondola, chifukwa dziko la pansi liri m'manja mwa munthu. Linapatsidwa kwa Iye ndipo iye anali wolamulira pamwamba pa chinthu chinachirichonse. Ndipo chilengedwe chonse chikubuma, kudikirira nthawi imeneyo imene pamene ana a Mulungu adzawonetseredwe kachiwiri. O, kalanga ine! Kuwonetseredwa kwa ana a Mulungu.

Tsopano. Ife ndi bwino kudzisiya izo pomwepano.

55 Koma a mithenga ali mu dzanja Lake la manja, kudikirira. Kwina kulikonseko kumene Iye amawatumiza iwo, iwo adzayankhula chinthu chomwecho, pakuti Mzimu Woyera umene unali mwa Khristu (O!), Mzimu umene unali mwa Khristu…. pamene iye ankachoka anati, “Kanthawi pang'ono ndipo dziko [”Kosmosi,“ liwu la chi Helene limene limatanthauza dongosolo la dziko. Osati dziko lapansi, dziko; dongosolo la dziko.] Siridzandionanso ine. Zipembedzo, kapena china chirichonse, sizidzandiwonanso ine; komabe inu mudzandiwona ine [Mpingo, wokhulupirira], pakuti Ine [Ine mlowa m'malo wadzina wa umwini, ndi zolondola], ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu mpaka mu

mathero a dziko; Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwa nthawizonse. Kodi inu mukuwona ichi?

56 Ndipo ngati uwo unali Mzimu Woyera wa Khristu unabwera pa tsiku la Pentekosite umene unachita zinthu zimenezo, iwo ndi Mzimu Woyera wa Khristu ukukankhiridwa kunja apa, Mzimu Woyera wa Khristu ukugwiritsabe apa, Mzimu Woyera wa Khristu ukugwirizitsabe pano, kupitirira mpaka apa, mpaka kumalekezero a dziko. Mzimu Woyera womwewo umene unamudzadza Paulo ndi Mzimu Woyera ndi zinthu zimene iye anachita, udzamudzadza uyu, Irenaeus, wodzadza ndi Mzimu Woyera, kumudzadza Martin wodzadza ndi Mzimu Woyera, ndi ena onsewo, odzadza ndi Mzimu Woyera, ndi kukudzaza iwe ndi ine kudzadza ndi Mzimu Woyera.

Ndipo ndi madalitso a chi Pentekosite kuchokera ku m'badwo wa mpingo umodzi kupita kwa wina: Alefa ndi Omega, mapeto ndi chiyambi ndi zonse; mudzu ndi mphukira ya Davide, nyenyezi ya ku m'mawa duwa la Rose wa Sharon, kakombo wa m'chigwa, ndi zina zonsezo; Atate, Mwana, Mzimu Woyera; Iye amene anali, amene ali ndipo adzabwera, Alefa, Omega; zonse mu zonse. O, kalanga ine! Zimene zingandipangitse ine kuimba nyimbo:

O, kodi inu mumanena kuti ine ndi ndani (ananena Yesu.),

Kodi inu mukuti ine ndinachokera kuti,

Inu mukuwadziwa Atate wanga, kapena inu mungatchule Dzina lake?

Iye ananena, Ine ndi Alefa ndi Omega, chiyambi

kuchokera ku mapeto,

Ine ndine chilengedwe chonse, ndipo Yesu ndiye Dzinalo.

Ine ndine amene ndinayankhula ndi Mose mu tsamba loyaka moto,

Ine ndine Mulungu wa Abraham, kuwala ndi

nyenyezi ya m'mawa. (Uko nkulondola.)

Ine ndine duwa la Rose wa Sharoni,

Kodi inu mukuti ine ndinachokera kuti?

Ine ndine chilengedwe chonse, koma Yesu ndiye Dzinalo.

57 Banja lonse la m'miyamba ndi dziko la pansi lamamagirizidwa ndi Dzina limodzi ilo lopezekeka pena paliponse, lodalitsika, lozadzidwa nd Mzimu Woyera, lotsamwidwa, lotchulidwa ndi Mzimu Woyera,

kuyankhulidwa ndi Mzimu Woyera, lobadwa ndi Mzimu Woyera. Chabwino. Mulungu anapereka ilo ku banja lonse kumwamba ndi dziko lapansi, ndi chinachirichonse… kuti bondo lina lirilonse ligwadire pa dzina limenelo. Ndipo palibe dzina lina lapatsidwa pansi pa thambo limene munthu angapulumutsidwe nalo. Osati “mwina,” “zikanakhala,” Koma “ayenera” kupumutsidwa nalo. O, ine ndikuzikonda zimenezi. Izi ndi zabwino. Chabwino.

58 Mu dzanja Lake la manja. Tsopano kodi inu mukuzipeza? Ndi mpingo wa Pentekosite - mphamvu, zizindikiro, zodabwitsa, zikuchitika paulendo wonse. Tsopano ife tiri… tayenda kudutsa mu mibadwo ya m'dima kumene unali pafupifupi kufafanizidwa.

Tsopano tiyeni titenge ndime yachiwiri iyi. Ayi, Ine ndikukhulupirira ife tingopitirira pang'ono chabe ndi ndime yoyamba apobe:

… Ine ndidziwa ntchito zako, kuti iwe amene uli nalo dzina kuti iwe uli moyo, ndipo ndiwe wakufa.

Titembenukire ku mpingo wotsatira apa. Inu mukupeza, “… koma iwe sunakane Dzina langa.” Mpingo wotsatira, “sunakane Dzina langa.” Koma mu Mpingo uwu, “… iwe uli ndi dzina.” Penyani apa. Mpingo uwu unausunga dzina lake. Mpingo uwu unasunga Dzina Lake. Mpingo uwu unasunga Dzina Lake. Ndipo Mpingo uwu unapita kudutsa mu m'badwo wa m'dima, ndipo panalibe kanthu kalikonse koyankhulidwa za ilo. Nthawi imene iwo abwera ku moyo kumbali iyi, oyambirira ochepa… opulumukayo, pamene Luther anawakokera iwo kunja, “Iwe uli nalo dzina kuti iwe uli wa moyo, koma iwe uli wakufa.

Tsopano, kodi ndi dzina liti limene iwo amagwiritsa ntchito pambuyo atasiya kugwiritsa ntchito Dzina la Yesu? Atate, Mwana, Mzimu Woyera, ndipo palibe chinthu chonga ichi. Icho ndi maphunziro a za umulungu akufa.

59 Ndiuzeni ine, Atate ndi dzina? Ndi Atate anagati ali muno? Kwezani dzanja lanu m'mwamba. Kodi ndi ndani wa inu amene amatchulidwa dzina Atate? Ana? Ndi anthu? Izi ndi zomwe izo ziri. Dzina lake si Mzimu Woyera - ndi zomwe izo ziri. Iwo ndi Mzimu Woyera. Dzina…Mzimu Woyera si dzina; Mzimu Woyera ndi udindo - Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.

Choncho inu mukuona, ichi changokhala ngati chopanda tsinde ngati umwana wa muyaya. Palibe chinthu chonga mwana wa muyaya mwana amabadwa kuchokera; cha muyaya sichitero.

60 Palibe chinthu chonga chomwechi, monga ine ndinanena usiku wina, monga Gahena wa muyaya. Inu mumapeza bwanji Gahena muyaya? Ndiye kuti apo pakhala pali Gahena nthawi zonse. Baibulo linanena kuti iyo inalengedwera mdierekezi ndi angelo ake. Apo nthawi zonse pakanakhala pali Gahena…. Ngati nthawi zonse ikanakhalapo, ndiyekuti ikanakhala iripo pachiyambi. Ndipo ndani amaigwiritsa ntchito iyo kumbuyo uko pamene Iye anali El, Elah, Elohim, m'modzi wodzikhalira yekha, pamene panalibe chinthu china chirichonse? Ndiyeno Gahena inali kukhala ndi iye kumeneko, mukuona. Gahena inapangidwira mdierekezi ndi angelo ake, ndi onse oipa adzaponyedwa mu iyo. Izo ndendende kulondola. Iwo adzalangidwa mwina kwa zaka ma miliyoni zana chifukwa cha zomwe iwo achita. Koma ikubwera nthawi imene iwo adzakhale ndi imfa yachiwiri. Palibe chinthu chimene chidzatsalire cha iwo. Chinthu china chirichonse chimene chinali ndi chiyambi chiri ndi mapeto. Choncho pamene ife tirandira moyo wa muyaya, ife tikulandira gawo la kuwala kwa kumwamba kumene kunalipo kumbuyo uko pasanakhale ngakhale kachidutswa ka mpweya. Kuwala kwa Mulungu kumabwera mu mitima mwathu kumene kukutiunikira ife kuti tione Yesu. Baibulo linanena ife sitikuona zinthu zonse, koma ife tikuona, Yesu.

61 Tsopano, Iye ananena, “Ine ndidziwa kuti … Ine ndi iye amene ali ndi Mizimu isanu ndi iwiri imene waitumiza ku mipingo isanu ndi iwiri ya. Ine ndidziwa zonse ntchito zako ndi zonse zokhudza izo, koma iwe uli nalo dzina kuti iwe uli wa moyo koma iwe ndi wakufa.” Tsopano, kumbukirani, kodi uwu unali m'badwo wa ndani? Martin Luther, m'badwo wa Luther.

Iwo anatsutsidwa pa chiyambi. Iwo analibe ngakhale chiyambi. Iwo anali akufa poyamba pomwe. Iwo sanali oti afe; iwo anali atafa poyamba pomwe, mwaona. Iwo anango “zembera kunja.”

62 Tsopano, zindikirani ichi. Tsopano, tiyeni tiwerenge ndime yotsatira: Penyani.

Kotero samala, ndipo limbikitsa zotsalazo, zomwe ziri pafupi kufa: kwa ine sindinapeze ntchito zako kukhala zangwiro pa maso pa Mulungu.

Tsopano, iye akuyankhula kwa Luther tsopano. Ife tonse tavomereza kuti uwo unali m'badwo wa Lutheran. Iwo unali kukonzanso. Tsopano kodi iye anati chiyani? “Inu munabweretsa dzina lonyenga kuti inu muli moyo, koma inu muli akufa.” Kodi iwo anachita chiyani? Iwo anaubwezeretsa iwo ku chipembedzo kawiri. Ndipo mphika sunganene ketulo kuda. Osafuulira pa Katolika, mwaona, chifukwa inu muli mwabwerera molunjika kwa iwo, kugwiritsa ntchito tidzikhulupiriro take tomweto, maina ndi….

Chabwino, Lutera anabweretsa anatulutsa katekisimu ambiri ndichina chirichonse chimene mpingo wa Katolika unali nacho, ndipo anadzitengera okha dzina, mwaona. “Inu muli ndi dzina lokuti inu muli ndi

moyo, koma inu mukuchokera ku ichi chakufa zaka chikwi pano, ndipo inu mukugwiritsabe dzinalo. Inu muli nalo dzina,” Kodi inu mukukumbukira? Kukhala otsimikiza kuti izi ndi zolondola, ku mipingo ina anati, “Inu mwakhala mwasunga dzina langa.” “Inu mwasunga dzina langa.” Mu m'badwo uno iwo analitaya ilo. Ndi kubwera apa ndi kunena, “Inu muli nalo dzina lina lokuti inu muli ndi moyo, koma inu muli akufa.”

63 O, inu a Methodisti, Baptisti, Presbaterian, Lutherani, ndi Pentekosite, lapani ndi kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu. Tulukani

kwa tizikhulupiriro ito takufa ndi zinthu zimene ziri za mpingo wa Katolika zomwe ziti zidzanyeketsedwe, ndi ana ake onse aakazi pamodzi naye. Palibe m'modzi angathe kunena kuti Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, iwo mtundu….

Ndipo chinthu icho chomwe iwo amachitcha Utatu Woyera! Utatu? Ine ndikufuna winawake apeze ngakhale liwu loti “Utatu” mu Baibulo, ndi kubwera kundiuza ine zokhudza ichi. Basi inu pezani liwu loti “Utatu” siriri nkomwe m'menemo. Palibepo chinthu chonga chimenechi.

64 Tsopano, “… ziri pafupi kufa. Gwiritsitsa chimene uli nacho. Luther anakukokerani inu kunja. Gwiritsani ku chimenecho, chifukwa icho chiri pafupi kufa. Iwo adzakukokerani inu kumbuyo ku icho kawiri. Gwiritsitsani icho. Icho chiri pafupi kufa.”

Tsopano, “… ndipo ine sindinakupeze iwe wangwiro pamaso pa Mulungu.” Kodi izo sizokongola? O, kalanga ine, Ine ndikuchikonda ichi. Osati wangwiro. Chifukwa chiyani? Iwo anali atangolungamitsidwa basi. Luther analalikira kulungamitsa. Inu munayenera kuyeretsedwa ndi kudzazidwa ndi Mzimu Woyera. Ndiyeno iwo sanali a iwo eni - iwo anapangidwa kukhala a ngwiro mwa Mzimu Woyera womwe unali mwa iwo.

Sim'khristu amene ali wa ngwiro; ndi Mzimu Woyera wa ngwiro womwe unali mwa iwo. Ucho ndi chomwe …. Monga ndinanena si phiri loyera; ndi Mulungu Woyera pa phiri. Osati mpingo woyera, osati anthu oyera; koma uwu ndi Mzimu Woyera mu mpingo ndi mwa anthu. Iyo ndi mbali yoyera, mwaona.

65 “Tsopano, ine sindinapeze ntchito zako zangwiro. Iwe sunafike kuungwiro.” Chifukwa ife tikupeza, tsopano, kuti iwo anali ndi kulungamitsidwa apa. Kulungamitsidwa. Ichi ndi… ayi, ine ndikupempha chikhululukiro chanu kulungamitsidwa kuli apa pansi pa Luther, ndipo kuyeretsedwa kuli apa, ndipo apa pali Mzimu Woyera. Mukuona?

Tsopano, izo zinthu zitatu zimene zinagwira ntchito mu mibadwo itatu ya Mipingo imeneyo, ndi zimene zikutengera kuti zikapange kubadwa kwa thunthu. Iwo anali atangotenga pakati ngati ka mbewu kakang'ono m'mimba mwa amayi (Uko ndi kulondola), Mzimu Woyera kubwera ku kubadwa.

66 Tsopano, ine ndikufuna ndikufunseni inu chinthu chinachake. Pamene kubadwa kwa chirengedwe kukuchitika, kodi chinthu choyambirira ndi chiyani kuchitika? Madzi. Chinthu chotsatira? Magazi. Kodi uko ndi kulondola? Chinthu chotsatira? Mzimu. Uko ndi kulondola. Kodi ndi chiyani chimene chinatuluka mu thupi la Yesu pamene Iye anafa? Iwo analasa m'mbali Mwake ndipo madzi ndi magazi zinatuluka, ndi “Ine ndikupereka Mzimu Wanga m'manja Mwanu.” Madzi, magazi, mzimu.

Choncho pamene tilungamitsidwa mwa chikhulupiriro (Aroma 5:1), ife tiri ndi mtendere ndi Mulungu kudzera mwa Ambuye Wathu Yesu Khristu. Kulungamitsa. Kuyeretsa, Aheberi 13:12 ndi 13, “Yesu anazunzika kunja kwa chipata kuti Iye akayeretse anthu ndi Magazi Ake omwe.”

Luka 24:49, “… koma inu kadikireni mu mzinda wa Yerusalemu mpaka inu mutadzazidwa ndi mphamvu yochokera kumwamba. Pambuyo pa izi Mzimu Woyera ubwera pa inu, pamenepo inu mudzakhala mboni zanga mu Yerusalemu, Yudeya, Samariya ….” Osati pamene inu mwakhala bishop, osati pamene inu mwakhala dikoni, osati pamene inu mwakhala m'busa, osati pamene inu mwakhala papa; koma “pambuyo pa izi, Mzimu Woyera, atabwera pa inu pamenepo inu mudzachitira umboni.”

Inu mutha kuchitira umboni kokha za mpingo wanu ndi kachikhulupiriro kanu, ichi ndi … ngati inu muli dikoni basi, ngati inu muli m'busa basi, ngati inu muli papa basi, kapena ngati inu muli …. Inu mukuchitira umboni kachikhulupiriro kanu. Koma pamene Mzimu Woyera ubwerapo, pamenepo inu mumachitira umboni za iyeyo. Ndipo ntchito zomwe iye anachita inu muchitanso, chifukwa moyo Wake uli mwa inu. O, O, kalanga ine, kalanga ine, ine ndikuzikonda zimenezo. Inde, bwana. O, Ine ndapeza zochuluka za ichi apa, ine ndikukhulupirira, koposa momwe inu mukuchitira kunja uko. Ine ndingodzimverera ubwino ndi ichi.

67 Zinthu zomwe ziri pafupi kufa, gwiritsitsanibe ku izo.“

Tsopano, iye akunena apa, tsopano mu ndime ya chitatu:

Kumbukirani tsopano umo unalandira niumva [ine ndikuzikonda zimenezo], ndipo gwiritsa nulape. Kotero ngati iwe siusamala, ine ndidzabwera kwa iwe ngati mbala, ndipo iwe siudzazindikira ora limene ine ndizadza pa iwe.

“Gwiritsani molimba kulungamitsidwa kwanu. Kakamirani ku ichi. Musalore anthu amenewo kuchimenyera icho m'mbuyo molimba kuchokera kwa inu. Chomwechonso chimene inu munalandira, inu munamva.”

Iwo amawerenga Baibulo lomweri limene ife timawerenga, mwaona. Koma iwo sanatenge zonse za ilo chifukwa sizinavumbulutsidwe kwa iwo. Izo sizinali za m'badwo wawo. Ichi ndi chifukwa chake iwo adzapezeke mu chiukitsiro. Iwo anayenda mu kuwala komwe iwo anayenera kuyendamo. Kotero iwo adzapezekamo.

68 Tsopano, ine ndinawamva anthu ambiri achi Pentekosite akulalikira ubatizo, akuti, “Iwo a chi Luther, ndi ena otero, sadzapezekamo.” O, inde. Inu mukudziwa kankhani kakang'ongo kokhudza Dotolo Aegery ku mtunda uko. Ine ndinamuuza iye….

Iye anati, “Kodi ndife yani?”

Ine ndinati… Inu mukudziwa, iwo anakuza seminale yayikulu ya chi Luther kumeneko, Betane, ku Minneapolis.

Ndipo iye anati, “Chabwino, kodi ife a chi Luther tiri ndi chiyani?”

Ine ndinati, “Chabwino, ine ndikuuzani inu. Ine ndikukhulupirira munali naye Khristu.”

Ndipo iye anati, “Chabwino, ife tikufuna Mzimu Woyera.” Iye anati, “Kodi inu mukuganiza ife tinali nawo iwo?”

Ine ndinati, “Mwakuyankhula kwina.” Ndipo ine ndinati, “Inu mukukhulupirira ku icho.”

Iye anati, “Chabwino, kodi inu mukutanthauza chiyani?

69 Tsopano, iwo ali ndi zikwi za maekala kumeneko kumene ophunzira awo…. Ngati iwo sangalipire maphunziro awo kumeneko, iwo amawasiya iwo kugwira ntchito kulipira maphunziro awo ndi kumadzala chimanga.

Ine ndinati, “Chabwino ….” Pali magome akulu basi. Iwo andipatsa ine limodzi mwa maphwando a zakudya za mitundu mitundu kumeneko, mu seminale yayikulu imeneyo. Iwo anali amuna abwino - Dotolo, Aegery atakhala apa, ndi m'bale Jack Moore pomwepano, chifukwa ine ndinakhala pafupi, kuti pamene iye alankhula mawu ena aakulu amene ine sindimawadziwa, ine ndikanam'menya Jack ndi mwendo wanga, ndi kuona zomwe iye ati anene, inu mukuona. Kotero ndiyeno ine ndinati ….

Iye anakhala moyandikana ndi ine, ndipo iye anati, “Chabwino, chomwe ife tikufuna kuti tichite ndi kupeza chinthu china chake pano.” Anati, “Ife tiri ndi njala ya kwa Mulungu.” Ndipo anati, “Ife tawerenga buku la a zachiPentekosite, mphatso.” Ndipo anati, “Ife tinapita, kagulu kathu ka abale kanauluka kupita ku Kalifoniya, ife tinakumana naye mwamuna amene analemba bukulo.” (Ine ndikumudziwa iye.)

Iye anati, “Ife tikufuna tiwone zina mwa mphatso zikugwira ntchito.”

Iye anati, 'Ine ndiribe ina iriyonse ya izo,' anati, 'ine basi ndinangolemba zokhudza izo,'“ iye anati.

Ndipo anati, “Ndiyeno pamene ife tinabwera chakuno ndipo ife tiwona izi, ife tiri ndi njala. Ife tikufuna Mulungu.”

70 Ndipo ine ndinati, “Chabwino, nthawi ina panali munthu anapita. [Inu mukudziwa, muzochita zake zomwe apo, mwaona.] Mwamuna anapita ndi kutipula munda waukulu wopambana. Ndipo iye anatenga mizu yonse kunja kwa ichi, ndi chinachirichonse, ndipo iye anadzala chimanga.

Mamawa wina uliwonse iye amapita pakhomo ndipo anayang'ana ngati iye anali ndi chimanga chirichonse. Chinthu choyamba inu mukudziwa, m'mawa wina, timasamba tiwiri tating'ono tinali tikutuluka. “Alipo amene anayamba walimapo chimanga …. (Kodi ali kuti George Wright ndi enawo, Roy Slaughter, ndi enawo? Inu mukudziwa, timasamba

tating'ono ito timene timatuluka.) “O,” iye ananena, “Mulungu alemekezeke chifukwa cha munda wanga wa chimanga.”

Ine ndinati, “Kodi iye anali ndi munda wa chimanga?”

Iye anati, “Chabwino, mu njira ina.”

Ine ndinati, “Mwakuyankhula kwina, inde.” Ine ndinati, “Awo munali inu a chi Lutheran mu kukonzanso koyamba kuika katsamba kakang'ono patsogolo apo, mwaona. Chabwino,” Ine ndinati, “Pang'ono ndi pang'ono chimanga icho chimakula.” Ine sindimuuze iye zokhuza “chomwe chinagwa,” inu mukuona. Ine ndinangomusiya iye adziwe kuti chimanga chinakula.

71 Kotero ine ndinati, “Chimanga chinakula, ndipo patatha kanthawi panabwera ngayaye pa icho. Ndipo ngayaye zimenezo zinayang'ana m'buyo pansi kwa tsamba ndipo zinati, 'Ha - ha - ha, Inu inu mulibe chiri chonse, inu a Chilutheran akale a miyambo; mwaona. Zinati, 'Ine ndi … Ine ndi amene ndi maberekesa nthawi yayikulu ya ma mishonale.'”

Mphepo inaomba, ndipo ngayaye zazing'ono zinagwa ngati choncho ndipo zinagwera pansi. Izo ndi Wesley, kuyeretsedwa, mwaona. Uwo unali m'badwo waukulu wa mishonale umene ife sitinayambe takhala nawo, unali mpingo wa Wesley, mu nthawi ya Wesley, mpaka kupitirira m'badwo uno. M'badwo wa mpingo wa Wesley. Unali m'badwo wa mishonale, ndipo unafalikira. Kodi iwo unachita chiyani? Iwo unafalitsa icho.

Mwaona, ngakhale chilengedwa chimachitira umboni wa zitatu izi, pomwepo. Chilengedwe pachokha. Mulungu pa chiyambi anapanga icho motero kuti chidzakhale choncho. Inu simukusoweka kukhala ndi Baibulo. Inu mutha kuyang'ana pa chilengedwe ndi kuona pamene inu muli.

72 Ndipo patapita kanthawi inagwa apo, kumeneko ndi chiyani chomwe chinaturuka? Apo pakubwera khutu la chimanga. Linali ndi njere pa ilo. Ilo linali gulu la a Chipentekosite. Tsopano, gulu la Chipentekosite linali mtundu womwewo wa gulu ili apa. Kuchokera kuno iye anali ndi timasamba tiwiri ta chimanga, Luther. Kuno iye anali ndi

ngayaye, Wesley, ndipo pansi kuno iye anali ndi njere ya chimanga. Chiyani? ndendende monga chinaliri kumbuyo kuno. Chinthu chomwecho.

Chabwino, tsopano, kodi ichi chinali chiyani kuno? Inu mukuti …. “Chabwino, tsopano,” a Chipentekosite anati, “Ine ndiribe nanu ntchito inu a Methodisti kapena inu a Lutheran.” Komabe, moyo womwewo umene unali mu timasambatiwiri tating'ono tinathandiza kupanga ngayaye. Ndipo moyo umene unali mu ngayaye unapanga chimanga. Choncho, inu mukuona ili lonse ndi dongosolo la Mulungu. Iwo anali ndi Mzimu Woyera, mwakuyankhula kwina. Koteronso Wesley pansi pa kuyeretsedwa. Koma lero unabweretsanso kuyankhula m'malirime ndi kubwezeretsa kwa pa chiyambi apa - Mzimu Woyera womwewo, inu mwaona, woonayo. Ameni. Inde.

73 Chabwino.

“Gwiritsitsa molimba chimene iwe unamva, kuopa chingafe.” Tsopano ndime ya chinayi, ine ndikukhulupirira ndi iyo.

Iwe uli nawo maina ochepa mu Sarde omwe sanadetse zovala zawo; ndipo iwo adzayenda ndi ine m'zoyera: chifukwa iwo ali oyenera.

Tsopano, osapanga chipembedzo kuchokera ku ichi. Ife sitikufuna kuchita zimenezo. (Ayi, Ine ndawerenga ndime yolakwika, kodi ine sindinatero? Kapena kodi ine ndatero tsopano? Eya, uko ndi kulondola. Eya chabwino. Eya.) “… mu Sarde … omwe sanadetse zovala zawo.” Analipo ochepa a iwo amene sanagwadirepo chinthu chimenecho, ndipo anazisungira iwo eni angwiro ndi oyera (nkukuluzi wakale kuchokera kumbuyo uko mpaka pa Pentekosite), odzazidwa ndi Mzimu.

Ambiri a iwo nthawi imeneyo mu m'badwo wa Luther anayamba kupanga chipembezo. Kodi iwo anachita chiyani? Anayamba kubwerera m'mbuyo monga Baibulo linanena, kuchita ngati mayi wawo. Kubwera m'mbuyo umo, anayambitsa chipembezo. Koma ochepa a iwo anaima molimba kuti iwo sakanachita icho. Iwo anakhala molondola kwa Mulungu. Anati, “Chabwino, ziribwino. Inu muli nawo maina ochepa, ndipo iwo ndi oyenera kuyenda pa maso pa ine. Atavala choyera. Musapange chipembezo. Musatenga

chiphunzitso cha Anikolayi, tsopano. Musayambe chipembezo chanu kachiwiri, koma tangokhalani mfulu mwa Mulungu. Lolani Mzimu Woyera utsogolere inu pamene inu mupitirira. Pali ochepa a iwo amene atsalabe.“

74 Tsopano ndime ya chisanu, ine ndikukhulupirira; “Iye amene ali nalo khutu, musiyeni iye….” Tiyeni tiwone tsopano:

Iye amene alakika, yemweyo adzamuveka zovala zoyera; ndipo ine sindidzalichotsa dzina lake Mubukhu la Moyo, koma ine ndidzavomereza dzina lake pamaso pa Atate Wanga, ndi pamaso pa Angelo.

Tsopano, maina ochepa, ochepa kwambiri, otsalira ochepa anatsala amene sanatenge pa … anatengedwa ndi chiphunzitso cha Chikatolika. Chabwino.

75 Tsopano ife tikubwera kuyankhula za kukonzanso. Ine ndikufuna ndi …. ine ndinasiya maziko a Lutheran kuti ine ndidzachipeze ichi muno. Tsopano ndime yotsatira inati: “Iye amene ali ndi khutu, amve chimene Mzimu unena kwa Mipingo.” Mulungu kuyesa kuwachenjedza iwo apa kukhala kunja kwa chi Nikolayi ichi: Kuti akhale kutali ndi uko; asunge zovala zawo zopanda banga kuchokera ku chinthu chirichonse cha pa dziko; basi angokhala mfulu mwa iye; ndipo Iye akanawatsogolera iwo ndi

kuwalondolera iwo. Tsopano, Icho ndi chiyambi choyamba.

76 Tsopano, pa “Kukonzanso” Ine ndikutanthauza opulumutsidwawo, omwe anapulumuka ngakhale mu mpingo wa Sarde. Kodi inu mukumvetsa chomwe ine ndikutanthauza? Iwo amene anapulumutsidwabe ku chinthu chonyasa icho. Tsopano, ife tidzazitenganso izo mawa usiku ndi kuchibweretsa icho molunjika mpaka mu m'badwo wa Pentekosite, ndi kukuwonetsani inu kuti chiri ndendende chomwecho.

Tsopano, pali zina za zinthu izi zomwe ife tinaziyankhula apa, zakuti kodi iwo anapulumuka bwanji ku chinthu ichi? Tsopano, ife tikuzitenga izo apa mu m'badwo wotsatira. Mwaona, ife tiyenera kuchitenga ichi apa kudzipanga izo kuyendera limodzi. Ngati inu simutero, ndiye inu mukuphonya kuwapatsa anthu … kuchikhomerera icho mu

m'badwo wotsatira, inu mukuona. Inu mungowasiya iwo akhale ndi ichi monga Baibulo laperekera ichi apa, mwaona. Chabwino.

77 Tsopano, opulumutsidwawo ndi amene Iye akuyankhula za iwo. Ndi awa apa, kagulu kakang'ono aka apa kamene kakukhala ndi moyo pa kulungamitsidwa. Tsopano penyani. Iwo anatuluka, iwo anawona kuwala. Luther anabwera bwino … pambuyo pa imfa ya Luther, osati Luther.

Luther sanapange bungwe; linali gululo iye atachoka. Wesley sanapange bungwe, linali gululo iye atachoka. Iwo oyambitsa akale a Pentekosite sanapange bungwe; linali gululo iwo atachoka. Awo ndi omwe amachita izi, mwaona. Ndi mpiti wachiwiri umene umachita ichi. M'ngelo weniweni wa kuwala sadzapanga bungwe. Inu mudzapeza pa m'badwo wa Pentekosite uwu chomwe chimachitikanso ku mapeto kwa bungwe, mwaona, pamene Mzimu Woyera uti uulule ichi kwa ife.

78 Tsopano, Iye anati, “Inu muli ndi kuwala kochepa kumene kwatsala, pang'ono chabe. Iko kuli pafupi kufa. kukuzirala. Iko ndi kulungamitsidwa basi. Iwo atha kukukankhira iwe mbali ina iriyonse. Iwe ulibe moyo wina uliwonse pakali pano, chifukwa iwe unatenga dzina lolakwika. Komabe iwe watulutsidwa, mwaona. Inu munapulumuka ku mpingo wa chi Roma. Inu mwapulumuka ku ziphunzitso zonse, ndipo inu mwatulukabe kufika uko.” Tsopano, inu mukuwerenga Baibulo lomwelo, tsopano, koma … Baibulo lomwelo limene limaphunzitsa Mzimu Woyera iye sanawatsutse pa chomwe anali nacho. “Tangogwiritsani ku izo mpaka ine ndibwera [mwaona]. Tangogwiritsani.

79 Tsopano, m'badwo wa mpingowu unayamba pafupifupi 1520, pamene mpingo wa Roman Katolika wa ponseponse unali pa chi indeinde. Umene unatha m'mpaka pa October 31 (ngati inu nonse mukulemba izi), October 31, 1570 A.D., pamene Martin Luther anakhomera Mfundo zake makumi asanu ndi anayi ndi zisanu pa khomo la kachisi mu Wittenberg, Germany. Ndipo kuchokera nthawi imeneyo kukonzanso kunayamba. Kodi inu mwamvetsa madeti amenewo? Lolani ine ndipeze ichi kachiwiri kuti inu mukhale otsimikiza. October 31, 1570, A.D., pamene Martin, Luther anakhomera Mfundo zake makumi asanu ndi anayi ndi zisanu pa khomo la kachisi ku Wittenberg, W - i - t - t - e

- n - b - e - r - g, Wittenberg, Germany. Kuyambira tsiku limenelo kukonzanso kunayamba. Moto unayamba kuuluka.

Iye anatsutsa mpingo wa Katolika umenewo, kuima pamenepo, icho chiri mu dzanja lake, monga choncho. Iye anati, “Ichi chingakhale Thupi Loyera la Khristu? Ndi ka mkate ndi ka vinyo pang'ono.” Ndi phwaa, iye anauponyera iwo pansi. Uko ndi kulondola.

80 Iye anautsutsa Mpingo wa Katolika ndipo icho chinayamba … apang'ono anatuluka nthawi imeneyo. Chabwino. Icho chinayamba.

Koma chinali mochuluka inali nkhondo ya mphamvu za ndale osati za mpingo weniweni woona, kwa muyeso wa Chikhristu. Iwo anangomenyera kokha ufulu wandale kuti atuluke mu mpingowo ndi kupanga mpingo wina. Iwo sanakonze kutuluka mu mpingo wa Katolika kuti abweretse Mzimu Woyera ndi mphamvu mu mpingo chifukwa, iwo anaukana iwo, mwaona. Unali msonkhano wa ndale. Izo ndi … ichi ndithudi chikugwirizana. “Iwe uli ndi dzina kuti iwe uli ndi moyo ndipo uli okufa.”

Mu mawu ena, iye anangobweretsa kunja chipembedzo choukira, izo ndichoncho. Iye anabweretsa mwana wamkazi kunja kwa mpingo. Kunja kwa … Iye anabweretsa ka hule kuchokera kwa hule lalikulu. Izo ndi ndendende zimene zinachitika. Iye anabweretsa Athaliah kuchokera kwa Yezebeli.

81 Tsopano, wina aliyense amene amawerenga kukonzanso amadziwa kuti izo ndi choncho, chifukwa iye basi mophweka …. Zochepa za zotsalira za mafano zao zakale ndi madongosolo zomwe … ndi miyambo, iye mophweka anaziphwatsula izo. Koma kunena za kubwedzeretsa Mzimu Woyera mu Mpingo ngati m'mene unaliri m'mbuyo apa, iye sanachite icho. Ayi, bwana.

Iyo inali ndewu ya ndale kuposa ndewu ya uzimu. Izo zinali ndale m'malo mwa Mzimu Woyera. Iye anali asanalowe mu Mpingo. O, m'bale! Iye sanabwerere m'mbuyo Iye akubweranso apa, osati pamwamba apo.

82 Tsopano, uku kunali kusonkhanira kwakulu kwa ndale, koma ichi sichinali kwa Malemba Oyera ndi Mzimu Woyera.

Iwo unali msonkhano wandale, umene …. Iye anachotsa zina mwa za mafano akale za mtanda, ndi “Tikuoneni, Maria” ndi zonse izo. Koma iye anatulukabe ndi bukhu la chitsime. Iye anatulukabe ndi ichi …. Kodi inu mumachitchula ichi kuti chiyani? Mapemphero opatulika, kapena kaya chinali chiyani uko - nthawi imene iwo apita ku m'mawa wa Pasika, ndipo m'mbusa akuwafunira iwo mafuno abwino a Khrismasi, inu mukudziwa. Sadzawaonanso iwo mpaka nthawi ya Khrismasi iye anatero, inu mukudziwa. O, msonkhano wa ulimbitso ndi umene ine ndikuyesa kuyankhula za iwo. Kuwatenga iwo ndi kuwapatsa ulimbitso iwo. Apatseni iwo m'gonero woyamba ndi ulimbitso.

Palibe chinthu chonga ichi ngati ulimbitso. Ulimbitso okhawo umene ukutchulidwa mu Baibulo ndi pamene Mulungu atsimikizira Mawu Ake ndi zizindikiro ndi zodabwitsa zikutsatira. Uwo ndiye ulimbitso umene ife tikufuna. Osati ulimbitso wokhala membala wa mpingo wa Lutheran; koma Mulungu akutsimikizira Mawu Ake mwa inu. “Ndipo Ambuye anagwira ntchito ndi iwo [Marko 16], kutsimikizira Mawu ndi zizindikiro zikutsatira.” Uko ndi kutsimikizira mpingo wa Chipentekosite. Uwo ndiye ulimbitso… Mulungu amadzitsimikizira iyemwini kuti ali ndi moyo, ngati Mulungu wa zozizwitsa mu mpingo, kuyankhula m'malirime, kutanthauzira malirime, ndi kuchita zinthu zomwecho iwo anachita pa chiyambi.

83 Kodi ine ndikukutopetsani inu? [Osonkhana akuyankha, “Ayi”.] Chabwino. Tsopano, zindikirani, iwo sanabweretse chitsitsimutso cha Mzimu Woyera; iwo anabweretsa m'badwo wa mpingo watsopano. Iwo anabweretsa otulitsidwawo, opulumukawo kuchokera ku utsogoleri wa chi Roma, kupanga utsogoleri wa Chiprotestant. Icho mdi chokhaco chimene iwo anachita. Analumpha kuchoka mchiwaya ndi kugwera pa moto, mwaona. Izo ndi zolondola, ndendende. Yezebeli anangobereka mwana wa mkazi basi.

Ndipo tsopano musaganize kuti ine ndingoyankhula izi kuti ndioneka wanzeru. Ine ndikuyankhula izi chifukwa Baibulo linanena choncho. Baibulo mu Chibvumbulutso 17, linati, “Iye anali mayi wa mahule.” Yesu ananena apa, “Monga momwe analiri Yezebeli, kotero iye adzakhala.” Ndipo iye anaika ana ake aakazi amene anawononga dziko limene linali losawonongedwa.

Tsopano, izo ndendende zomwe Chiprotestanti chachita kwa Mzimu weniweni wa Mulungu. Chinayipitsa chinthu ichi, ndi kuika ichi kubwerera mu bungwe lina. Chimene, ngati Mulungu alola, Lamulungu m'mawa, ine ndikufuna ndikuwonetseni inu kuti iwo apanga fano kwa chirombo, ndipo chirombo chinali Roma. Ndipo iwo anapanga fano ngati choncho. Kodi ichi chinali chiyani? bungwe! O, ine ndikuyembekeza izo zikulowa mozama m'kati mwa mitima ya wanthu.

84 Tsopano inu mukudabwa chifukwa chomwe ine ndakhala ndikumenyena ndi mabungwe molimba choncho moyo wanga wonse. Inenso sindimadziwa. Koma chinali chinthu chinachake mkati mwanga, chikufuula. Ine sindikanachitira mwina.

Ine ndinadabwa. Nthawi zonse ndinadabwa chifukwa chiyani ine nthawi zonse ndimawasutsa azimayi motero, mwaona, moyo wanga wonse. Ichi si …. Ine sindikutanthauza akazi enieni. Ine ndikutanthauza awa oyera - kukhala, inu mukudziwa - amene makhalidwe a chirengedwe anaphwasuka mwa iwo, ndi chinachirichonse, inu mukudziwa. Uwo ndi mtundu ine … chinthu chinachake mwa ine. Nthawi imene ine ndinali m'nyamata wam'ng'ono, wakale, woonda uko, ndi kuwawona akazi awo kubwera akuyenda mu msewu, ndi kudziwa kuti amuna ali ku ntchito…. Ndi iwo apo kumeneko ndi mwamuna wina, ataledzera, m'mbali mwa nsewu. Ndipo amaperekeza iwo kuyenda kukwera ndi kutsika mumseu, kuwapangitsa iwo kuti kuledzera kuthe kuti akafike kunyuma ndi kuwaphikira amuna awo chakudya cha madzulo.

Ine ndinati, “Iwo sakuyenera chipolopolo chabwino kuti chikalowe mwa iwo.” Uko ndi kulondola. Ine ndinati, “Iwo ndi otsikitsitsa kuposa nyama kuchita chinthu ngati chomwecho.”

Ndipo ine, pamene ndinali ndi zaka khumi ndi zisanu ndi ziwiri, zaka khumi ndi zisanu ndi zitatu, ine ndikawona msungwana akubwera akuyenda mu msewu, ine ndinkaolokera kupita tsidya lina la msewu. Ine ndinati, “Njoka yonunkha iyo,” mwaona. Ndipo ine ndikanakhala m'dani weniweni. Koma pamene ine ndinalandira Mulungu mu mtima mwanga, Mulungu analola ine ndidziwe kuti iye ali nazo ngale zina kunja uko. Iye

ali ndi ma madona ena enieni. Iwo onse sadzaziwononga iwo eni monga choncho. Ndikuyamika Mulungu chifukwa cha izo.

85 Nthawi imene ine ndinali uko mu Afrika, pamene ine ndinali mu Switzerland, pamene ine ndinali mu Rome ine ndinafunsidwa funso ili, “Eya. Nena, M'bale Branham, kodi inu nonse mulibedi akazi ena ake abwino mu Amerika? Nyimbo ina iri yonse imabwera kuno, mumakhala chinthu china chake choipa chokhudza azimayi anu.”

Ine ndinati, “Awo ndi achiMerika. Koma ife tiri ndi Ufumu wina umene ulipo kumeneko. Uwo ndi Ufumu wa Mulungu. Iwo ali madona enieni mpaka mkati.” Iwo ali.

86 Baibulo linati, apo mu … m'neneri anati …. Ine ndikukhulupirira unali pafupifupi mutu wa chisanu wa Yesaya, ine sindiri wotsimikiza. Ukanatha kukhala mutu wa 5 kapena wa 6 kumeneko, kuyankhula za, “Wodala iye mwana wamkazi wa Ziyoni adzapulumuka mu tsiku limenelo kuchokera ku zinthu zonse izo.” M'mene iye ati adzayendere kudutsa mu msewu, Iye akanadzatsitsa m'munsi masokosi ake; ankanyag'ama pamene iye ankayenda, kuzipotokola monga choncho, ndi zinthu zomwe iye amakhoza kuchita. Ndendende njira yomweyo iwo akuchita tsopano, mwangwiro basi. Kuvala zovala ngati mwamuna, chimene chiri chonyasa kwa Mulungu.

87 Ine ndinawona gulu la za chipembedzo kanthawi kapitako, kupita mkati kukakhala ndi mtundu wina wa zophulitsa makombola iwo amachita pafupifupi usiku wina uliwonse. Ndipo akazi awa onse kumapita m'menemo ndi makabudula … kapena kodi paja zinthu izi iwo amazitchula chiyani? Osati makabudula, koma zinazo. Eya, mathalauza othina olekeza pamwamba pa phazi ovalidwa ndi okwera njinga za mpikisano, kapena zinthu izo kumeneko. Iwo akufunika phazi litakankhidwa chabwino. M'bale ilo ndi thabwa lotambalala choncho. Uko nkulondola. “Phazi” kuchokera ku liwu loti “Woyenda pansi.” Apo ndi kuyenda ndi mapazi ako. Ndipo ndi ndendende zomwe iwo akufuna. Uko nkulondola. Koma, o, inu mukuti, “Chabwino, tsopano ine ndikuganiza ndi zolemekezeka kwa mkazi kuvala zimenezo kuposa kuvala siketi.”

Mulungu anati, “Ndi chonyazisa m'maso mwake kwa mkazi kuvala chovala ….” Ndipo pamene mkazi adula tsitsi lake ngati mwamuna …. Mulungu amafuna mkazi azioneka ngati mkazi, adzivala ngati mkazi adzichita ngati mkazi.

88 Ndipo Iye safuna mwamuna ndi tsitsi lake lalikulu likulendewera pansi ngati chonchi, ndi angati bakha wakhala pambuyo pa mutu wake ngati choncho. Iye amafuna iye aziwoneka ngati mamuna. Inde, bwana. Kalanga ine, iwo amavala mwachikazi kwambiri mpaka iwo sadziwa nkomwe kuti kuti ndi aamuna kapena aakazi.

Ndizomvetsa chisoni, izi zonyasa ndi zinthu zina ziri zonse ife tiri nazo lero. Ndi zosadabwitsa ife tikukhala ku mapeto a nthawi. Palibe chinthu chimene chatsalira mu dziko koma Mulungu kuti atsanulire mkwiyo wake pa ili ndi kuliotcha ilo. Ndi zimenezo basi. Mulungu wolungama ndi woyera sangachite chirichonse koma chimenecho.

Iwo anakana magazi a Yesu Khristu. Iwo anazipangira ziphunzitso iwo eni. Iwo alowa mu bungwe. Ndipo wakale… m'bambo woyera wina kale ali ndi … wosakwatira wa kale ndi kolala yake yotembenuzidwa, kubwera apo ndi kuwauza iwo, “Ana anga odalitsidwa.” Izo zikutanthauza koposa nkhumba kunena izo.

Ine ndikukuuzani inu chomwe ife tikusowa lero ndi kubwerera ku Baibulo ndi Mzimu Woyera, m'bale, ndi mphamvu ya Khristu oukitsidwayo kubwera mu Mpingo kumachita zizindikiro ndi zodabwitsa ndi zozwitsa. Ameni! Uwo ndi Uthenga wabwino. Inde.

89 Anabweretsa patsogolo …. Kotero …. Inde, izo ndi zolondola, icho chinachita. Chitsitsimutso chinachita zinthu zina zabwino zokongola, chitsitsimutso chimenecho. Koma ichi sichinabweretse Mzimu Woyera. Iwo sanabweretse iwo [Mzimu Woyera] apo mpaka kufika mu m'badwo wa Pentekosite uwu. Koma ichi chinachita chinthu chimodzi. Chitsisimutso ichi chachita zinthu zina zimene Iye anati, “Musalore ichi kuti chife tsopano. Chirimbitseni ichi, pitirizani kuwonjezera ku ichi.” Mwaona?

Icho chinabweretsanso Baibulo la ulere kwa anthu. M'badwo wa Luther unabweretsa Baibulo la ulere. Iwo anapanga nyumba zodindira mabuku ndi kuyamba

kupereka Baibulo kudziko. Mulungu adalitse achi Lutheran pa izo. Inde, bwana. Iwo aika Baibulo kubwerera mu dzanja la osonkhana kachiwiri. Ilo linali kwa wansembe yekha basi. Samaloledwa nkomwe kuliyang'ana ilo, chifukwa chinali chimene papa ananena. Iye anali mulungu, kotero chinachirichonse chimene iye amanena, icho chimachitika.

90 Kotero tsopano, chitsitsimutso cha Lutheran, chiyani … iwo amafuna ku chirimbitsa.

Tsopano inu muli ndi Baibulo m'manja mwanu. Tsopano werengani ilo! Khulupirirani ilo. Osangolisiya ilo apo pa shelefu, kunena, “Chabwino, ife tiri ndi Baibulo.” Izo sizidzakuchitirani, inu ubwino kumeneko. Pali ambiri achi Lutheran mu Pentekosite lero, akulisiya Baibulo, ndi kutenga zomwe winawake wanena zokhudza ilo. M'bale, werengani Mawu! “Fufuzani Malemba, chifukwa iwo ndi amene akuchitira umboni za ine,” anatero Yesu. “Mwa iwo mukuganiza inu muli ndi moyo wa muyaya.” Icho ndi chinthu choti mudzichita - werengani Mawu.

Tsopano, Iye anati, “Gwiritsani kwa icho ndipo musalore icho kupulumuka.”

91 Ndipo chinthu china chimene Iye anafuna kuti iwo agwiritse, chomwe chinali ndi mphamvu pang'ono zinatsatira mwa icho, chinali…. Chitsitsimutso cha Lutheran, chinthu chachiwiri chomwe ichi chinachita, chinabweretsa chiphunzitso cha kulungamitsa ku kuwala. Akatolika satenga kulungamitsidwa. Iwo ndi mpingo wa Katolika…. Monga wansembe uja, iwo anamudula iye akuyankhula pa wayilesi kuno nthawi

zina zapitazo. Iye anati, “Palibe chipulumutsa kwina kulikonse koma mu mpingo wa Katolika.” Chipulumutso chiri mwa Khristu - osati mu mpingo wa Katolika, osati mu mpingo wa chi Protestanti. Chiri mwa Khristu - chipulumutso.

Koma Akatolika amakhulupirira …. Iwo sasamala chimene Baibulo limanena. Ndi zimene mpingo ukunena, mwaona. Siungayankhule kwa iwo, chifukwa palibe mpata wotero. Palibe njira yoyankhulira nawo. Iwo sasamala. Iwo ali nazo…. Iwo adzayankhula kwa inu pa bukhu lawo la Chitsime, chinthu china ngati chimenecho. Koma chikabwera ku Baibulo, iwo basi amangochitaya icho; Ndi zimene mpingo unena.

92 Yesu ananena, mu chinthu chomwechomwechi, Yesu Iyemwini anati ngati munthu wina achotsa china chirichonse kapena kuwonjezera chinthu chinachirichonse ku ichi Iye adzachotsa gawo lake mu buku la Moyo. Yesu ananti, “Lolani mawu amunthu wina aliyense akhale a bodza, ndi anga akhale woona. Miyamba ndi dziko lapansi zidzachoka koma Mawu Anga sadzachoka.” Kodi uku ndi kulondola? O, ndi zimenezo, m'bale. Ine ndi wokhulupirira Mawu a Mulungu. Uko ndi kulondola.

Ndipo si Mawu okha amene Mulungu wayankhula kumeneko, ndipo ine ndifunsa Atate akumwamba kuti andipatse ine Mzimu Woyera kuti ukatsimikizire Mawuwo, ku mupanga Khristu kukhala mwa ine - pa icho ine ndikudziwa kuti ndiri ndi moyo wa muyaya. Osati chifukwa ine ndikuyenera ichi; chifukwa chisomo chake chapereka ichi kwa ine. Ilo ndi thanthwe. “Pa nthanthwe ili ine ndidzamangapo Mpingo wanga,” Iye ananena.

93 Chabwino, Kulungamitsa. Chabwino.

Chinthu cha ichi chinali, pambuyo pakuti iwo atabweretsa chirichonse chomwe iwo samaloredwa kuti achisiye icho chife - icho chinali, iwo anali ndi Baibulo m'manja mwawo kachiwiri. A chi Lutheran anachita izo. Ndipo chinthu china, iwo anali ndi chiphunzitso cha kulungamitsidwa mwa chikhulupiriro. Ndi chimene Luthera anaphunzitsa. Wina aliyense akudziwa izo. Icho chinali chiphunzitso chake. Kulunga …. Kodi simungathe inu kuwona momwe izo ziriri za ngwiro? Ndipo kenako akubwera Wesley ndi kuyeretsedwa. Ndipo apa akubwera a Pentekosite ndi ubatizo wa Mzimu Woyera mwangwiro basi.

94 “Tsopano, inu muli ndi zinthu zochepa. Gwirizitsani kwa izo tsopano, ndipo osalora izo zife. Ngati inu simugwiritsitsa pa izo, ine ndidzabwera mwamsanga ngati mbala ndipo inu mudzapita m'mbuyo kulowa mu chipembedzo kachiwiri.” Ndipo izo ndi zimene iwo anachita, basi ndendende. Anabwereramonso. Inu mudzabwerera m'mbuyo ku chi Nikolayi kachiwiri, chifukwa inu mudzabwereranso kulowa mu chipembedzo. Gwiritsitsani. Pitirirani kuwerenga Baibulo limenelo, ndi kupitirira kulungamitsidwa, ndi kupita chitsogolo mokangamira“

Koma panali otsalira ochepa omwe anatuluka umo, otsalira ochepa. Kuchokera poyamba anabwera Luther, kenako anabwera Zwingli, ndi kupitirira mpaka; Calvin, ndi

ena otero, kufikira kwa Wesley. Koma panali otsalira ochepa otuluka kumeneko amene anaphunzitsa kuyeretsedwa. Ndipo kuchokera kwa oyeretsedwa akubwera otsalira ochepa amene analowa mu Mzimu Woyera. Onani awo otsalira ochepa njira yonse kumeneko akusunga izo za moyo. Chabwino.

95 Koma, chachitatu, iwo anabweretsa ziphunzitso zambiri za maonekedwe a chikunja pamodzi nao … ndi ichi: Monga ngati zipembezo; ubatizo wonyenga (tsopano iwo akutuluka akukonkha, ndi zina zotero ngati zimenezo, ndi Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera.); iwo anabweretsa bukhu la chitsime. Moona anali nazo … moona iwo anakwanira ndi dzinalo … ndi chimene Yesu ananena apa, “Iwe uli nalo dzina lakuti uli ndi moyo, koma ndiwe wakufa.” Uko ndi kulondola. Chabwino.

96 Chachinayi, ndi zoona kuti kukonzanso kunasesera kutali zambiri za mafano awo opukutidwa bwino, ndi miyambo, ndi zina zotero. Koma chinalephera - mu mpingo, mu kubwezeretsa kobweretsapo kukonzanso - ichi chinalephera kubwezeretsa chiphunzitso cha uthenga wabwino wa mphumphu ndi zizindikiro zikutsatira.

Mpingo wa Lutheran siunakhale nacho ichi. Iwo sanakhalepo nacho icho, ndipo iwo sanakhalepo nacho ichi mu m'badwo wa Wesley. Iwo anakhala nacho kokha ichi ku mapeto kwa m'badwo wa Laodikaya uwu. Tsopano, pamene ife tifika mu uwo, ine ndizabwerera mu Malemba ndi kukuwonetsani inu ndendende m'mene iwo analonjezera icho. Iwo analibe … sanabweretse chitsitsimutso cha Mzimu Woyera.

97 Iwo anatembenuka kuchokera ku mafano, ndi …. Iwo anatembenuka kuchoka ku mafano, izo ndi zoona. Iwo anachotsa mafano mu mpingo - Maria, ndi Yosefe, ndi Petro, ndi Paulo, ndi onse a iwo. Iwo anatembenuka kuchoka ku mafano, koma iwo sanatembenukire kwa Khristu woukitsidwa. Luther anawatembenuzira iwo kuchoka ku mafano, koma kulowa mu chofananirako ngati ndale, kapena chipembezo, kapena bungwe - kuzipanga iwo eni basi bungwe lina, fano ngati loyamba lija ndi kuyesa kukulitsa ilo ndi chipembezo.

Ndipo tsopano iwo ali akumenyabe. A Methodisti akufunabe onse a Baptisti akhale a Methodisti. Ndi

onse a Lutheran akufuna onse a Baptisti ndi a Methodisti akhale a

Lutheran. A Pentekosite akufuna onse a Baptisti, a Luthera, ndi china chirichonse kuti akhale a Pentekosite. Mwaona, ichi kungopitirira kuonjezera ku chipembezo chanu.

Koma ilo si dongosolo la Mulungu kuyambankuyamba. Dongosolo la Mulungu pa kubwezeretsa linali kubweretsanso izo zomwe zinali pa chiyambi.

98 Tayang'anani. Ukitsani icho. Ngati buku ili ligwa pansi …. tsopano, kutenga bukhu lina pa kutenga malo ake icho si kubwezeretsa, chiukitsiro. Inu muyenera kubweretsa lomwero apo. Ameni. Choncho ngati Mpingo unafa kudzera mu Mibadwo ya M'dima ndipo ndi kukhala wachikunja wathunthu apa, kenakono kubwezeretsa …. Uko ndi kukonzanso, kukonza. Koma kukonzedwa ndi kubadwa kachiwiri ndi zinthu ziwiri zosiyana, mwaona. Iwo anabweretsa kukonzanso, kukonza, kuchoka ku zochuluka za mafano awo ndi zina zotero, koma iwo sanabweretse Mzimu Woyera mu mpingo. O, lidalitsike Dzina la Ambuye! M'bale, mlongo, kodi mukutha inu kuona ichi?

Iwo sanabweretse Mzimu Woyera chifukwa iye amene abweretsa kuwala kwenikweni kwa uthenga wabwino woona (valani chisote chanu tsopano), m'modzi amene amabweretsa kuwala kwa uthenga wabwino woona ndi m'ngelo wa mpingo cha apa. Tsopano, ife tikhala tikuona izo Lamulungu.

99 Tsopano, iwo adzakhala ndi kuwala ndi kuwala pa pamwamba pa kuwala, ndi kuwala kwa m'Khristu, koma wina aliyense wa iwo adzabwerera kulowa mu bungwe ilo.

Koma padzabwera wina amene adzaime motsutsa iye. Inde, bwana! ndipo iye adzawakoka otsalira kuchokera kumeneko monga motsimikiza ngati m'mene ine ndaimira pa guwali. Uko ndi kulondola. Ndipo iye adzapita molunjika kuchiyambi. Ndipo ine ndidzatenga Malemba kuchokera mu Chipangano Chakale ndi Chipangano Chatsopano ndi kutsimikizira kwa inu kuti Iye adzachita izo - M'ngelo wa Mpingo wa Laodikaya. Uko ndi kulondola, kupita molunjika kumbuyoku chiyambi, ndi kuukitsanso chinthu ichi apa. Ndipo chiukitsiro chidzabwera pa tsiku la ichi apa. Uko ndi kulondola.

100 Koma Luther anaukokera Mpingo kunja, “wopulumukawo,” wopulumukawo - mphondero imodzi, kuyere … kulungamitsidwa. Wopulumutsidwawo. Inu mwatuluka

phazi limodzi kuchoka mu chikunja. Izo zonse ndi zolondola. Nthawi yotsatirayo icho chidzatuluka mapazi awiri. Izo ndi zonse kungokhala ngati ….

Kodi inu munazindikirapo mu Baibulo, panali madzi akubwera kutuluka kuchokera kumbuyo kwa Kachisi? Ndipo iye anati anaona madzi akukwera kufika mu mawondo ake; ndipo madzi otsatira kukwera mpaka mu chiuno mwake, ndi nthawi yotsatira anakwera kupitirira mutu wake. Koma pamene iye anapita mopitirira mutu wake, iye amayenera kufika pa malo oti iye akanatha kusambira, mwaona. Iye amayenera kusambira. Kotero ife tikulowa m'malo tsopano, oti ndi mwina kusambira kapena kumira. Izo ndi zonse. Ichi chidzakumizani inu, ndi kukukokololerani inu mwathunthu kutali, kapena kukubweretsani inu mkati, chimodzi. Kotero, ndi kusambira kapena kumira! Aleluya!

O, ine ndine wokondwa chifukwa cha Mzimu Woyera. Kodi inu simuli? Ine ndiri wokondwa kuti ine nditha kunena ine ndine m'modzi wa iwo.

Ndine m'modzi wawo … (Kodi ndani iwo?

Osati ichi, icho, kapena icho, kapena icho.)

Ine ndine wokondwa kuti nditha kunena kuti ndine m'modzi wawo;

Aleluya!

M'modzi wawo, m'modzi wawo,

Ine ndine wokondwa kuti ine nditha kunena ndine m'modzi wawo.

101 Kodi izo sizikumveka bwino? Mvetserani:

Iwo anasonkhana mu chipinda chapamwamba,

Onse kupemphera mu Dzina lake,

Iwo anabatizidwa ndi Mzimu Woyera,

Ndipo mphamvu ya utumiki inabwera;

Tsopano zomwe Iye anachita kwa iwo tsiku limenelo,

Iye adzachita kwa iwe chimodzimodzi,

Ndine wokondwa kuti nditha kunena ndine m'modzi wawo.

O, m'modzi wawo, ndine m'modzi wawo,

Ndine wokondwa kuti ine nditha kunena ndine m'modzi wawo;

Aleluya!

M'modzi wawo, m'modzi wawo,

Ndine wokondwa kuti ine nditha kunena ndine m'modzi wawo.

Kodi iwo amapita ku ma seminale? Ayi. Ena a iwo sangathe ngakhale kulemba dzina lawo lomwe. Uko nkulondola. Petro samatha Baibulo linati Iye anali mbuli ndi munthu wosaphunzira, Iye ndi Yohane. Koma iwo amakhala tcheru kumvetsera kwa iwo, chifukwa iwo anadziwa kuti anakhala ndi Yesu.

Ngakhale anthu awa ali osaphunzira

(Ophunzira),

Kapena kudzitukumula ku kutchuka kwa dziko (“O, Mulungu adalitsike,

ine ndiri nao ambiri akutiakuti.“),

Iwo onse analandira Pentekosite wao,

Anabatizidwa mu Dzina la Yesu;

Ndipo iwo akulengeza tsopano, konse kutali ndi kofalikira.

Mphamvu yake idakali yomweyobe.

Ndine wokondwa kuti nditha kunena ndine m'modzi wawo;

M'modzi wawo, m'modzi wawo,

Ndine wokondwa kuti nditha kunena ndine m'modzi wawo.

102 Kodi inu simuli wokondwa ndi ichi? Wokondwa kwambiri kukhala m'modzi wawo. Ine ndibwino kukhala m'modzi wa iwo kuposa chinthu china chirichonse chimene ine ndikudziwa. O, ine ndibwino kukhala m'modzi wa iwo kuposa kukhala Pulezidenti wa United States, kapena kukhala mfumu ya dziko.

Ngati Ambuye Yesu akanayenda pansi pano, kunena, “Ine ndikutembenuzira iwe m'mbuyo ku zaka makumi awiri, ndi kukupanga iwe woyang'anira , kapena mfumu, ya dziko lonse , ndi kukupatsa iwe zaka zikwi khumi za moyopa dziko iri la pansi, kukhala wa zaka makumi awiri - osakhala ndi tsiku lodwala, matenda a mtima, ndi zonse

zidzakhala chimwemwe ndi china chirichonse, ndi mfumu ya dziko lonse lapansi, kukhala ndi moyo zaka zikwi khumi; kapena, inu mukufuna kudzakhala m'modzi wa iwo, ndi kungokhala nako kuvutika mopitirira monga inu mukuchitiramu?“, Ine ndidzanena, ”Ndine wokondwa kuti nditha kunena ndine m'modzi wawo.“

Kodi patatha pa zaka zikwi khumizo, chizachitikeno nchiyani? Koma uwu ndi muyaya. Kodi iwo unabwera bwanji, abale? O, iwo wakhala … kubwera kudzera m'magazi. Uko ndi kulondola. Wabwera kuchokera kutali, ndipo wabwera ndi Mulungu kupangidwa thupi ndi kukhala pakati pathu.

103 Modyera ng'ombe kale lapitalo, ine ndikudziwa ichi ndi indedi choncho,

Mwana anabadwa kupulumutsa anthu kuchokera ku machimo awo.

Yohane anaona iye pagombe, Mwanawankhosa

Kwa nthawizonse,

O, Khristu, wopachikidwa wa pa Kalivale.

O, ine ndimamukonda mwamuna uyo wochokera ku Galileya,

wochokera ku Galileya,

Pakuti Iye wachita zambiri kwa ine.

Iye wakhululukira machimo anga onse, Waika

Mzimu Woyera mwaine;

O, ine ndimukonda, ine ndimukonda mwamuna ameneyo

wochokera ku Galileya.

Mkazi pa chitsime, Iye machimo ake onse anachita anamuuza,

(Iye ali yemweyo dzulo, lero ndi kunthawizonse.)

Momwe analiri ndi amuna asanu.

Iye anakhululukidwa ku tchimo lirilonse, ndipo mtendere

Wozama unaikidwa mwa iye;

Iye analira, “Bwerani mudzaone mwamuna uyu wochokera ku Galileya!”

O, ine ndimukonda mwamuna uyo wochokera ku Galileya, wochokera ku Galileya,

Pakuti Iye wachita zambiri kwa ine.

Iye anakhululukira machimo anga onse, kuikamo

Mzimu Woyera mwaine;

O, ine ndimukonda, ine ndimukonda mwamuna uyo wochokera ku Galileya.

Wamisonkho anapita kukapemphera mu Kachisi kumeneko tsiku lina,

Iye analira, “O, Ambuye mukhale wa chifundo kwa ine!”

Iye anakhululukidwa kwa tchimo lina lirilonse, ndi mtendere

Wozama unabwera mwa iye;

Iye anati, “Bwerani mudzaone mwamuna uyu wochokera ku Galileya.”

(Ine ndikuzikonda izo, kodi inu simukutero?)

Olumala anapangidwa kuyenda, osayankhula

anapangidwa kuyanthula,

Mphamvu inayankhulidwa ndi chikondi pamwamba pa Nyanja;

Ndipo akhungu anapangidwa kuona, ine ndikudziwa ichi

Chikanakhala kokha

Chifundo cha mwamuna uja wochokera ku Galileya.

Imbani iyo ndi ine:

O, ine ndikumukonda mwamuna uyo wa ku Galileya, wa ku Galileya,

Pakuti Iye wachita zambiri kwa ine.

Iye anakhululukira machimo anga onse, Kuikamo

Mzimu Woyera mwaine;

O, ine ndimukonda, ine ndimukonda mwamuna uyo wa ku Galileya.

104 Kodi inu simukuchikonda ichi? O, kalanga ine! Uthenga wabwino uwu wa Mzimu Woyera, o, momwe ine ndikuukondera iwo! Ine ndimukonda iye ndi mtima wanga wonse. Ndipo ine ndine wokondwa usiku uno kuti ine ndawerengedwa ndi iwo, ndipo tiri limodzi ngati abale ndi alongo. Baptisti, Methodisti, apresi … Katolika, a Presbateria, ndi ena onse, Mulungu watibweretsa ife kuchokera mbali zosiyanasiyana, ndipo watibweretsa ife kuno ku chiyanjano chachikulu ichi cha Mzimu Woyera.

Osakhala wa chipembedzo chirichonse (izo ndi ziri kwa iwo momwe akuchitira), koma ife tiri mu ufumu wa chinsinsi. Ife tabatizidwa kulowa mu thupi la chinsinsi la Yesu Khristu ndi Mzimu Woyera. Ameneyo ndi ndani? Wa Methodist, Baptist, Presbateria ndi amene afuna: muloreni iye abwere. Ndipo Yesu anati, “Onse amene Atate andipatsa ine adzabwera kwa ine. Palibe m'modzi wa iwo adzataike, ndipo ine ndidzawaukitsanso iwo pa tsiku lotsiriza.” O, kalanga ine!

Ife tinkaimba nyimbo yakale pa guwa kuno. Ine sindikudziwa ngati ife tingathe kuimba iyo kapena ayi. “Chipinda, chipinda, inde, pali chipinda. Pali chipinda pa kasupe cha ine.” Inu mukonda nyimbo zakale izo

monga choncho? Tipatseni ife poyambira pa piyano, winawake, ngati pali wina amene akudziwa kuiyambitsa iyo. Kodi alikuti woimba piyano wathu? Kodi iye ali pano? Kapena ndi … M'bale Teddy, kapena wina wa iwo pano? O, kalanga ine! Ine sindikumuona iye malo ena aliwonse.

Chipinda, chipinda, inde, pali chipinda,

pali chipinda pa kasupe cha inu;

Chipinda, chipinda, inde, pali chipinda,

Pali chipinda pa kasupe cha inu.

105 Kodi inu mumakonda izo nyimbo zakalezo? Ndipo ine ndimakonda iyinso:

Pa mtanda pamene Mpulumutsi Wanga anafera,

Pansi kumeneko kuyeretsedwa kuchokera ku tchimo ine ndinalira;

O, pamenepo ku mtima wanga magazi anayikidwa;

Ulemerero kwa Dzina lake!

Ulemerero kwa Dzina lake (Dzina lake la mtengo wapatali)!

O, ulemerero kwa … (tiyeni tingotseka maso

athu tsopano, ndi kuimba iyo.)

O, pamenepo ku mtima wanga magazi anaikidwa;

Ulemerero kwa Dzina lake!

Ine ndapulumutsidwa modabwitsa ku tchimo,

Yesu mokoma akukhala mkati mwanga,

Apo pamtanda pomwe iye anandirandira;

Ulemerero kwa Dzina lake!

Ulemerero kwa Dzina lake (Dzina ilo la mtengo wapatali)!

Ulemerero kwa Dzina lake (Dzina la mtengo wapatali)!

Apo ku mtima wanga magazi anayikidwa;

Ulemerero kwa Dzina lake!

Tsopano pamene ife tiyimba ndime yotsatirayi, gwiranani chanza ndi winawake ali ku tsogolo kwanu, kumbuyo kwanu, m'mbali mwanu.

Bwerani kukasupe uyu wolemera ndi wokoma;

Ponyani moyo wanu wosaukawo pa mapazi a Mpulumutsiyo;

O, dumphirani umo lero, ndi kupangidwa wa mphumphu.

Ulemerero kwa Dzina lake!

Ulemerero kwa Dzina lake (Dzina ilo la mtengo wapatali)!

Ulemerero kwa Dzina lake la mtengo wapatali!

Apo ku mtima wanga magazi anayikidwa.

Ulemerero kwa Dzina lake!

O, ine ndikuzikonda izo. Kodi inu simukuzikonda?

Ulemerero kwa Dzina lake (Dzina la mtengo wapatali)!

Ulemerero kwa Dzina lake!

Apo ku mtima wanga magazi anayikidwa.

Ulemerero kwa Dzina lake!

O, kalanga ine! Ine ndine wokondwa kwambiri chifukwa cha izo, kodi inu simuli? Wokondwa kwambiri kuti ine nditha kubwera kukasupeUyu wolemera ndi wokoma, kuponya moyo wanga wosauka Pamapazi a Mpulumutsiyo.

106 Ine ndikukumbukira tsiku lina pamene ndinali mnyamata wam'ng'ono, wa zaka pafupifupi khumi, zisanu ndi zitatu, ndikuthawa kwa Mulungu. Ine ndinapita cha ku madzulo. Bambo wanga anali wokwera hatchi, ndipo ine ndinafuna kupita uko ndi kukagonjetsa ma hatchi. Panali chinthu chinachake chinali ndi njala mu mtima mwanga. O, ine ndikukuuzani inu! Ine ndinapita uko kwa mlaliki wa Baptisti. Iye anati, “Imira, ndi kungonena 'Yesu ndi Mwana wa wa Mulungu'. Ife tiika dzina lako pa bukhu.”

Zimenezo sizinandikwanire ine. Kwina kulikonse kumene ine ndinapita, winawake …. Wa Seventh - day Adventist, ndinapita kukamuona iye - mwamuna wabwino, M'bale Barker, m'bale wokondedwa. Iye anati, “Billy, bwera ndi kuvomereza sabata la Ambuye.” (Ine ndiri nalo tsopano.) koma iye anati, “Tsiku la sabata.”

Ndipo ine ndinaganiza, “O, kalanga ine! Izo basi sizikuonekabe ngati ndi icho ….”

107 Ine ndinapita uko ku madzulo, ndipo ine ndinaganiza …. Ndinafika kumbuyo uko usiku umenewo. Ife tinali pa kusonkhanitsa. Ndipo inu mukudziwa, inu mumachotsapo chokhalira chanu, ndi chikwama chanu, ndi kuziika izo pansi; ndipo mumagwiritsa ntchito chokhalira chanu, ngati pilo. Ndipo ine ndinagona chafufumimba pansi pa mitengo ya payini yakaleyo usiku umenewo. Ine ndinali kulondera masana, ndipo kotero anyamata a usiku anali akutuluka kubweretsa ng'ombe kumusi.

Ndipo panali bambo wina wokalamba wotchedwa “Slim” wochokera ku Texas. Iye anali ndi gitala pamenepo, ndipo iye amalisewera: “Ulemerero ku Dzina lake.” Ndipo munthu wina pamenepo anali ndi chipeso ndi kachidutswa ka pepala, akumayimba mouzira mpweya mu icho. [M'bale Branham akung'ung'udza,“ Ulemerero kwa Dzina lake.”] Iwo anakhala akuimba nyimbo zina, nyimba za anyamata woweta ng'ombe, ndipo amaimba iyo “Pansi pa mtanda.” Kalanga ine!

Ine ndinatembenuka, kuika chofunda changa pa mwamba pa mutu wanga ngati chonchi. Ine ndinayang'ana m'mbuyo uko, inu mukudziwa. Chinawoneka ngati nyenyezi izo zinali zikulendewera pansi pansi pamenepo, chifupi ndi pa mwamba pa mitengo imeneyo ndi mapiri amenewo. Mu zonong'ona zosatha zakale izo mapayini awo ine ndimatha kumumva iye akukuwa, “Adamu, kodi iwe uli kuti?”

108 Pafupi masabata atatu pambuyo pa izo, ine ndinapita mu mzinda ndipo anyamata onse anali ataledzera. Ndipo ine sindinamwe, ndipo ine ndinali kuti ndiwatenge iwo onse kunyumba kukawasanjikiza iwo mu galimoto mulimonse. Iwo anatuluka kunja uko, ndipo amawomberana pa zala za wina ndi mzake, ndi china chirichonsecho - zinali zoopsa kukhala wotetezeka. Kujambula mzere woongoka pansi kudutsa apo, ndipo amatchova juga wina ndi mnzake ya madolla asanu iwo amatha kuyenda pa iwo; ndipo iwo samatha kuyenda mwa m'mbali pamenepo monga choncho, inu mukudziwa. Ndi izo ndi m'mene zinaliri, mpaka iwo onse mowa utawathera, iwo atatha kupeza ndalama zawo.

Ndipo ine ndinali kumeneko, ndipo iwo onse amamwa. Ine ndinapita ku malo ochezera ndi kukhala pansi. Ine ndinaganiza, “Kalanga ine, kalanga ine!” pafupifupi zaka makumi atatu ndi zisanu zapitazo, kapena … makumi atatu ndi zisanu, ine ndikuganiza - zaka makumi atatu ndi zisanu zapitazo. Ndipo ine ndinakhala pansi pamenepo motalikira.

Phoenix anali malo aang'ono nthawi imeneyo. Ife tinkachokera ku Wickenburg, kumusi uko. Ine ndinakhala pansi apo, ndipo panali mtsungwana wam'ng'ono wa ku Spain amayenda kudutsa pamenepo; ndipo ine, kukhala pamenepo ndi chipewa changa chachikulu ichi chitakhala kumbuyo kwa mutu wanga. Iye anadutsa, ndi kugwetsa kampango kakang'ono ka m'manja aka, inu mukudziwa.

Ine ndinati, “Eh! Inu munagwetsa mpango wanu wa m'manja.” Ine ndinalibe chidwi.

109 Ine ndinamva kaphokoso kakang'ono ku musi mu msewu kumeneko, ndipo ndinapita kumusi kumeneko. Ndipo panali mnyamata wachikulire, anatembenuzidwa zinyumba zosungiramo ma hatchi kumeneko pankhope pake pali zipsera za nthomba, ndipo misonzi ikutsetsereka m'masaya mwake pamenepo, akusewera gitala, akuimba,

“Ulemerero kwa Dzina lake!” O, kalanga ine! Misonzi ikutsetserekera m'musi mwa nkhope yake, iye anaima ndi kunena, “Abale, iwe siumadziwa cimene icho chiri, mpaka iwe utalandira, Khristu wodabwitsa. Ulemerero kwa Dzina lake!”

Ndipo ine ndinakokera chipewacho m'munsi, ndipo ine ndinachokapo! O, kalanga ine! Inu simungabisale kwa Iye. Inu basi mungotuluka, ndi kumuvomereza Iye. O, Iye ndi wodabwitsa, inde, Iye ali.

Ine ndapulumutsidwa modabwitsa ku tchimo,

Yesu mokoma kwambiri akukhala mwa ine (akukhala mwa ine),

Apo pa mtanda pamene Iye anandirandira ine.

Ulemerero kwa Dzina lake!

Ulemerero kwa Dzina lake!

Ulemerero kwa Dzina lake!

O, pamenepo ku mtima wanga magazi anayikidwa.

Ulemerero kwa Dzina lake!

O, bwerani kukasupe uyu wolemera ndi wokoma;

tangoponyerani moyo wanu wosauka pa mapazi a Mpulumutsi;

O, zigwetserenimo lero, ndi kupangidwa wa mphuphu;

Ulemerero kwa Dzina lake!

Tsopano tiyeni tiweramitse mitu yathu. Tangokwezani m'mwamba manja anu tsopano:

(Ulemerero kwa Dzina lake (ulemerero, ulemerero))!

O, Mulungu, Dzina la mtengo wapatali!

Apo ku mtima wanga magazi anayikidwa;

Ulemerero kwa Dzina lake!

110 Ulemerero kwa Mulungu! Tiyeni tiimirire kamphindi chabe tangodikirani, dikirani. [Mlongo wina akuyankhula ndi lirime lina. M'bale akupereka kutanthauzira: “Eyaa, anthu Anga, Ine ndayankhula ndi inu usiku uwu monga inu mwasonkhana pamodzi, ngakhale Ine ndayenda pa mitima yanu usiku uno, ndipo ndalasa moyo wanu ndi Mzimu wanga

ndi Mawu Anga. Ine ndikuyankhulanso, ana Anga. Inde, masiku amene aikidwa patsogolo pa inu adzakhala masiku akulu kwa iwo amene adzalengeze kutsatira Ine, atero Ambuye. Chifukwa Ine ndinena kuti ndidzawalitsira pa njira yanu zinthu zambiri zochokera m'Mawu Anga.

“Ndipo ndayankhula kwa inu, anthu Anga, kuti ngati, inu mudzalinga kunditsata Ine, ndiyeno Ine ndidzapereka kwa inu nzeru za kumvetsetsa mu zinthu izi. Pakuti pamene Ine ndikuyang'ana pakati panu usiku uno, Ine ndikuwona kuti chiripo m'mitima mwa ena, atero Ambuye, kuti alipo ena usiku uno, Ine ndinena kwa inu, amene akuvutika kuti iwo azakhulupirira chiyani.

“Koma anthu Anga usiku uno Ine ndikuyankhula kwa inu: inu musakhale ofooka. Ndipo inu musachoke pa malo ano, Ine ndinena, ndi mitima yakugwa ndi malingaliro ku zinthu izi. Chifukwa Ine ndinena kwa inu kuti ngati inu mudzayang'ana kwa Ambuye, Ine ndikunena kuti Ine ndizakupatsani inu kumvetsetsa, ndipo Ine ndidzachita ndi inu monga m'mene Ine ndichitira mwana. Ndipo Ine ndidzabweretsa inu kulowa mu kuwala kwa zinthu zomwezi.

“Ndipo, Ine ndikunena kuti Ine ndidzakupangitsani inu kukhala angwiro monga anthu Anga, ndipo Ine ndikuyankhula kwa inu, ana Anga amuna ndi akazi, usiku uno, pamene inu mukuchoka pamalo ano. Ndipo pamene inu mukupita ku malo ambiri kumene inu munachokera, Ine ndikuti kodi inu mungatenge kuwala uku, ndi kukakhala mboni ya ichi kwa anthu ambiri? Pakuti Ine ndikunena kuti kuzungulira dziko la pansi usiku uno kuli mdima ndi chisokonezo. Koma Ine ndikuyankhula kwa antchito Anga, usiku uno kwezani kuwala kwa choonadi cha uthenga Wanga wabwino. Eyaa, lengezani Mawu Anga oyera kwa anthu Anga kuti iwo akamasulidwe kuchokera ku zinthu zonse izi, atero Ambuye.”]

Tsopano, ngati pangakhale ena amene sangadziwe kuti icho ndi chiyani, icho ndi chiPentekosite, Mzimu Woyera kuyankhula. Yesu ananena, “Pitani mu dziko lonse, kalalikireni Uthenga wabwino. Zizindikiro izi zidzawatsata iwo amene akhulupirira. Iwo adzayankhula ndi malirime atsopano, adzaika manja pa odwala, iwo adzachiritsidwa.” Zinthu zonse izi zimene iye wayankhulazi, zizafika pochitika.

O, ine ndine wokondwa kwambiri. Kodi inu mwawona Mzimu Woyera, kubwera kutsimikizira Mawu amenewo? Kuwala, tengani iko musakayikire iko. Tangolandirani ichi, ndipo Iye adzachita ndi inu monga mwana, ndi kukukwezani inu m'mwamba. Kodi izo sizokoma za Mzimu Woyera? - Mzimu Woyera pa ife.

Ine ndikukumbukira nthawi ina mu Baibulo, iwo sankadziwa kuti njira iti yomwe chinthucho chibwerere. M'dani anali kubwera ndipo Mzimu Woyera unagwera pa munthu ngati choncho, ndi kuwawuza iwo basi ndendende koti iwo apite. Ndipo iwo anapita kumeneko, ndipo Mulungu anasokoneza gulu lina la ankhondolo, ndi kuwalozera koti iwo apite. Uko ndi kulondola. O, ife tikukhalabe m'masiku a Baibulo, sichoncho? Ameni. Nthawizonse, pokhapokha ngati Mzimu Woyera uli kumeneko.

111 O, tiyeni ife tiimirire pamene ife tikuimba:
Tenga Dzina la Yesu ndi iwe
(kumbukirani Uthenga),
Mwana wachisoni ndi wa tsoka;
Lidzakasangalatsa iwe ndi kukupatsa chitonthozo,
Litenge ilo kwina kulikonse iwe upita.
Dzina la mtengo wapatali (dzina la mtengo wapatali),
O, lokoma motani (o lokoma motani).
Chiyembekezo cha dziko ndi chimwemwe cha kumwamba;
Dzina la mtengo wapatali (Dzina la mtengo wapatali ilo),
O, lokoma motani!
Chiyembekezo cha dziko ndi chimwemwe cha kumwamba.
Tengani Dzina la Yesu ndi iwe,
Ngati chishango ku msampha uliwonse;
Pamene mayesero akuzinga iwe,
Puma Dzina ilo loyera mu pemphero.
(Mulungu akwezeke!)
Dzina la mtengo wapatali (Dzina la mtengo wapatali),
O, lokoma motani! (O, lokoma motani)!
Chiyembekezo cha dziko ndi chimwemwe cha kumwamba;
Dzina la mtengo wapatali (Dzina la mtengo wapatali),
O, lokoma motani!
Chiyembekezo cha dziko ndi chimwemwe cha kumwamba;

112 Mvetserani ku ndime iyo:
Tengani Dzina la Yesu ndi iwe,
Ngati chishango ku msampha uliwonse;
Pamene mayesero akuzinga iwe,
Puma Dzina ilo loyera mu pemphero.
O, tiyeni tiimbe iyi kachiwiri;
Tengani Dzina la Yesu ndi iwe,
Ngati chishango ku msampha uliwonse;
amene mayesero akuzinga iwe,
Puma Dzina ilo loyera mu pemphero.
Tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano:
Dzina la mtengo wapatali (Dzina la mtengo wapatali),
O, lokoma motani!
Chiyembekezo cha dziko ndi chimwemwe cha kumwamba;
Dzina la mtengo wapatali, O, lokoma motani!
(O, lokoma motani!),

Chiyembekezo cha dziko ndi chimwemwe cha kumwamba

www.messagehub.info

Maulaliki wolalikidawa ndi

William Marrion Branham

"...mu masiku a liwu..." Chivumbulutso 10:7